

Tsiku la Mapemphero a Amayi pa Dziko Lonse

March 7, 2020

Kukhala ndi Khalidwe Labwino mu Dziko Loipa

[Kupemphedwa Kusenza Mtanda]

Mulinso maphunziro a chigawo cha masana

Mtima Umene Mulungu Amakondwera Kukhalamo

[Ubwino wa Kusweka ndi Kudzichepetsa]

Zolembedwa ndi Melody Mason



Zokonzedwa ndi Nthambi ya Mautumiki a Amayi ku Likulu la Mpingo wa Seventh-day Adventist
padziko lonse (General Conference) 12501 Old Columbia Pike, Silver Spring, MD 20904-6600
USA

Otanthauzira

Malawi Union Conference, Women's Ministries department

Contact

Mrs Emily Banda Egolet

Mtsogoleri wa Amayi komanso Ana ku Malawi



Kuchokera ku Likulu la Mpingo

(General Conference)



UTUMIKI WA AMAYI

28 October, 2019

Okondedwa Alongo,

Landirani moni wachisangalalo. Tsiku la Mapemphero a Amayi pa Dziko Lonse lafikanso. Pamene mukukonzekera tsikuli, konzani dongosolo lokhala ndi nthawi yambiri yamapemphero sabata limodzi tsikuli lisanafike komanso sabata limodzi pambuyo pa tsikuli. Pemphero ndi gawo lofunikira mu ubale wathu watsiku ndi tsiku ndi Yesu. Pemphero limatifikitsa chifupifupi ndi mpando wachifumu wa Mulungu ndipo limatilimbikitsa. Mu pemphero tikhozakuuza Mulungu nkhwaza zathu zonse, ngakhale zinthu zimene sitingathe kuuza munthu wina aliynse padziko lapansi. Mzimu Woyera amatenga mapemphero athu ndi kumufotokozera Atate m'mawu amene amanena zoono zenizeni za mu mtima mwathu.

Pa tsikuili la Mapemphero tikukupemphani kuti “. . . mupemphere nthawi yonse mwaMzimu, ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtimaonse” (*Aefeso 6:18*). Tonsefe timapempherera mabanja ndi abwenzi athu koma Tsiku ili la Mapemphero tidzakhala ndi nthawi yopempherera awo amene sitikuwadziwa-atsogoleri a boma (atchuleni maina awo), atsogoleri a mpingo aku ma konferensi athu, osowa pokhala, akazi amasiye, ana ovutika ponseponse, amene akuzunzidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo, iwo amene akukhala okha, amene akuchitiridwa nkhanza. . . Mndandandawu ukupitirirabe. Onjezerani mmene mwaonera. Mukhoza kuonjezera gulu limodzi limene lalembedwa pa mdandandanda wa

mapemphero a tsiku lililonse. Pemphereraninso iwo amene ali osadziwika ndi ooneka onyozeka kwa inu amene Mulungu akuwaitanira kuti akhale a pabusa Pake.

Utumiki wathu pa tsiku ili la mapemphero wamanga nthenje pa kukhala ndi khalidwe labwino. Posatengera zomwe tikudutsamo kapena zikoka zomwe zatizungulira ife, tikupemphedwa kuti tikhale molingana ndi khalidwe lomwe Yesu anationetsera. Kunena mosapsatira mawu, kukhala ndi khalidwe labwino zili ngati kukhala monga anakhalira Yesu. Izitu sizichitika popanda kulimbika m'pemphero komanso ntchito ya Mzimu Woyera. Chipatso cha Mzimu Woyera ndi umboni woti mtima wabwino ukupangidwa kukhala molingana ndi chifanizo cha Yesu

Ndi pemphero lathu kuti uthenga umenewu ndi zonse zili m'menemu zikulimbikitsani kuti pemphero likhale gawo la dongosolo lanu la tsiku ndi tsiku lotsatira Yesu, ndikukhala monga Yesu pang'ono ndi pang'ono.

Madalitso ndi chimwemwekwainu,

Ndine



Heather-Dawn Small, mtsogoleri

12501 Old Columbia Pike, Silver Spring MD 20904-6600 USA • Office (301) 680 6608 • women.adventist.org

Za m'katimu

<i>Ziyang'aniro za Pemphero.</i>	<i>4</i>
<i>Zokhudza Mlembi.</i>	<i>5</i>
<i>Zolembe zokhudza Chilinganizo.</i>	<i>5</i>
<i>Ndondomeko ya Utumiki.</i>	<i>6</i>
<i>Nthano ya Ana</i>	<i>7</i>
<i>Ulaliki.....</i>	<i>11</i>
<i>Chilinganizo cha Sabata Sukulu.</i>	<i>21</i>
<i>Chilinganizo cha Lasabata Masana.</i>	<i>28</i>
<i>Maphunziro a Chigawo cha Masana.</i>	<i>29</i>

Ziyang'aniro za Pemphero

Mu zilinganizo zathu lero, tiphunzira za kukhala ndi khalidwe labwino mu dziko loipa, tiphunziranso kupemphera pogwiritsa ntchito zinsinzi khumi ndi ziwiri zolandirira mphamvu yochokera kumwamba, pambali pa izi tipemphedwa kuti tisiye khalidwe lathu lonyada ncholinga choti tikhale odzichepetsa. Ellen G. White, mayi wa pemphero komanso chikhulupiriro, akutilimbikitsa motere:

“Yesu amatiuza moonekeratu kuti kupempha kwathu kukhale molingana ndi chifuniro cha Mulungu; tiyenera kupempha zinthu zomwe lye anatilonjeza ife, ndipo chilichonse chomwe talandira chiyenera kugwiritsidwa ntchito pochita chifuniro Chake. Ngati tachita izi, lonjezo (la kuyankhidwa kwa pemphero) lidzakwaniritsidwa” (*Prayer*, tsamba 101).

“Kunyada nkosafunika, kumatilepheretsa kusalandira madalitso a Khristu osalekeza amene lye anadza kudzapereka” (*Steps to Christ*, tsamba 30).

“Moyo wa Khristu wationetsa zimene munthu akhoza kuchita pokhala ndi khalidwe la umulungu. Ifenso tikhoza kulandira nawo zonse zimene Khristu analandira kuchokera kwa Mulungu. Tsono pemphani ndi kulandira. Pokhala ndi chikhulupiriro chosafoka monga cha Yakobo, ndi kulimbika mtima monga Eliya, landirani zomwe Mulungu anakulonjezani” (*Christ's Object Lessons*, tsamba 149).

Chaka chino chidwi chathu chili popempherera kudzichepetsa kwakukulu, chikhulupiriro cholimba, ndi khalidwe labwino longa la Khristu.

- Dzipempherereni nokha komanso mboni yanu
- Pemphererani banja ndi ana anu
- Pemphererani banja ndi okondwedwa anu
- Pemphererani ziwalo za mpingo zomwe mumasonkhana nazo
- Pemphererani abusa ndi akulu anu a mpingo
- Pemphererani atsogoleri anu a boma

Pemphereraninso ma division a mpingo ali m'munsiwa, kuphatikiza amayi, ndi atsogoleri a utumiki wa amayi.

- East-Central Africa Division
- Euro-Asia Division
- Inter-American Division

- Inter-European Division
- North American Division
- Northern Asia-Pacific Division
- South American Division
- South Pacific Division
- Southern Africa-Indian Ocean Division
- Southern Asia Division
- Southern Asia-Pacific Division
- Trans-European Division
- West-Central Africa Division

Zokhudza Mlembi

Ulaliki: Kukhala ndi Khalidwe Labwino mu Dziko Loipa

Melody Mason (wodziwikanso ndi dzina loti Melodious Echo) amakonda komanso kuchita chidwi ndi Yesu ndinso kuthandiza anthu ena kuti akhale pa ubale wabwino ndo ndi Khristu. Mayiyu ndi mlembi wa bukhu lokondedwa kwambiri lotchedwa *Daring to Ask for More: Divine Keys to Answered Prayer*, lomwe linamasuliridwa mu ziyankhulo khumi. Zambiri zomwe zalembedwa mu masamba cholemba ichi chokhudza Tsiku la Mapemphero a Utumuki wa Amayi Padziko Lonse zatengedwa mu bukhu la Mayi Mason lomwe lituluke posachedwa lotchedwa *Daring to Live by Every Word: Divine Keys to Abundant Living*.

Mayiwa pakadali pano amatsogolera mapemphero otchedwa United Prayer a ku General Conference ndipo amathandizanso kupititsa patsogolo ntchito ya Kutsitsimuka ndi Kukonzanso mu mpingo wa Seventh-day Adventist padziko lonse. Iwo aonekapo kangapo konse mu ma pologalamu osiyana-siyana pa kanema ya Hope Channel komanso kanema ya 3ABN, ndipo maphunziro komanso maumboni awo amapezeka pa makina a intaneti, YouTube. Iwotu amakonda kulemba, kukwera mapiri, kukwera njinga, kuyendera zachilengedwe, akapezanso mpata, nthawi zina amakachita ntchito ya umishonale m'maiko ena. Pakadali pano akukhala ku Silver Spring Maryland m'dziko la United States of America.

Maphunziro: Mtima umene Mulungu Amakondwera Kukhalamo

Pamene tikukonzekera ulendo wakumwamba komanso kupemphera kuti titsitsimutsidwe, kodi tiyenera kukhala ndi makhalidwe otani? Yesaya 57:15 akutiyanika. “Pakuti atero lye amene ali wmatali wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lake ndiye Woyera, Ndikhala m'malo atali ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzichepetsa, kutsitsimutsa mzimu wa odzichepetsa, ndi kutsitsimutsa mtima wa osweka.”

M'maphunziro a masana, Mayi Mason akutilimbikitsa kuti tiyang'ane pa Malembo pamene iwo akutifotokozera za mtima umene Mulungu amakondwera kukhalamo. Iye amakhala mu mtima wodzichepetsa, wosweka, ndi mtima wotamanda umene umapereka ulemu waukulu kwa Mulungu

Ndondomeko ya Utumiki (Ndondomeko ya Kupembedza Yomwe Tangoiyerekeza)

Kuitanira ku Kupembedza

Lemba Lotsogolera: 2 Petro 1:3, 4

Vesi 3- Popeza mphamvu ya umulungu wake idatipatsa ife zonse za pamoyo ndi chipembedzo, mwa chidziwitso cha Iye adatiitana ife ndi ulemerero ndi ukoma wake wa Iye yekha.

Vesi 4-Mwa izi adatiipatsa malonjezano a mtengo wake ndi akulu ndithu; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nawo umulungu wake, mutapuluma ku chivundi chili pa dziko lapansi m'chilakolako.

Nyimbo ya matamando: 162 "Yesu Anditsogozatu" (Khristu mu Nyimbo)

PempheroLoyamba:

Zopereka:

Kuwerenga Kovomerezana: Sankhani nyimbo kuchokera mu Khristu mu Nyimbo

Nthano ya Ana:

Nyimbo yapadera:

Mutu wa Ulaliki: "Kukhala ndi Khalidwe Labwino mu Dziko Loipa"

Nyimbo Yomaliza: Sankhani nyimbo kuchokera mu Khristu mu Nyimbo

Pemphero Lotsiriza:

Nthano ya Ana

M'mene Larisa Anaphunzirira Kusala kudyā ndi Kupempherera

(Nthanoyi yatengedwa m'bukhu la Adventist Mission)

Kodi ndi angati mwa inu munakhalapo osadya chakudya? Nzovutatu kukhala ndi njala, si choncho?

Nthawi zina anthu amasankha kuti asadye chakudya ncholinga choti akhale ndi nthawi yambiri yopemphera. Iwo akachita izi, zimatchedwa kuti “kusala kudyā.”

Kodi mukudziwa kuti Mulungu amatiuza kuti nthawi zina tiyenera kusala kudyā-izi zikutanthauza kuti timayenera osadya chakudya komanso kusiya kuchita chinthu china kwa kanthawi, ndi cholinga choti tikhale ndi nthawi yochuluka popempherera chinthu china chofunikira kwambiri.

M'mawa uno ndikufuna kukuuzani za mtsikana wina wachichepere wa zaka 13 wotchedwa Larisa, wa m'dziko la Czech Republic, amene anaphunzira kusala kudyā ndi kupemphera.

Makolo ake a Larisa amasala kudyā nthawi zonse pamene pali chinthu chinthu chomwe chawadetsa nkhwana.

Bambo ake akakumana ndi vuto lalikulu kuntchito kwawo ku Prague, iwo ndi akazi awo samadya chakudya tsiku lonse. M'malo mwake, amangomwa madzi kwinku akupemphera kwa Mulungu zokhudza vuto la kuntchitolo.

Agogo a mtsikanayu akakumananso ndi chobetchera chilichonse chachikulu, makolo ake samadya chakudya tsiku lonse, m'malo mwake amangodya zipatso ndi zamasamba uku akupempherera za vuto la agogo lija.

Madzulo wina, nthawi ya mapemphero, bambo ake a Larisa analengeza ku banja lonse (kwa amayi ndi ana atatu) kuti azakhali awo wokondedwa amafuna kulekana ndi amuna awo. Bambowa ndi akazi awo anaganiza kuti asale kudyā tsiku lotsatiralo.

Apa Larisa anayankhula:

Iye nati, “Nanenso ndisala nawo kudya.”

Bambo ake anapukusa mutu kenako anati:

“Ine ndi mayi ako takuuzapo kangapo konse kuti iweyo udakali wachichepere mwakuti sungakwanitse kukhala tsiku lonse osadya.”

“Komatu Adadi musaiwale kuti ndili ndi zaka 13 pano. Musayese ndine kamwana kazaka 9 kapena 5 monga alili achimwene angawa awiriwa. Nanenso ndikufunitsitsa nditasala kudya ndi kupempherera nawo azakhali,” anapempha motero Larisa.

Makolo ake sankadziwa kuti atani ndipempho la mwana wawoyi, koma iye anapitirizabe kuwapempha.

Kenako mayi ake anabweretsa ganizo loti Larisa adzasale nawo kudya koma azizangodya zipatso zokha basi ndi zamasamba. Koma Larisa anakanitsitsa nanena kuti akufuna kusala kudya koti asadyenso kalikonse monga amachitira makolo ake. Pamapeto bambo ake anamulola, Larisa anapita kukagona ali wokondwa.

Kutacha anakukumbukira kuti akuyenera kusadya kanthu kalikonse tsiku lonse koma angathe kumwa madzi okha ndiponso amayenera kupemphera pafupi-pafupi kuti azakhali ake asinthe ganizo lawo lofuna kulekana ndi amuna awo.

“Chonde Ambuye ukwati umenewu usathe, chitanipo kanthu, ndikudziwa kuti palibe chokulakani inu, ndipo ndikudziwa kuti mukhoza kuwathandiza azakhali anga,” anapemphera motero Larisa.

Atangomaliza kupemphera anadzuka namwa madzi.

Banja lonse linasonkhana nachita mapemphero a mmawa kuphatikizirapo kupempherera azakhali aja.

Pamene achimwene ake a Larisa awiri amathamangira ku khitchini kuti akatenge chakudya cha mmawa, iye anathamanga kupita ku chipinda kwake, analowa natseka chitseko ncholinga choti asaone anawo akudya. Anawerenga Baibulo napemphereranso azakhali ake aja kuti achotse ganizo lofuna kulekana ndi amuna awo. Atamva achimwene ake aja kuti akudyabe, Larisa anatenga bulashi yopentera napenta chithunzi cha mitengo itali-itali yobiriwira komanso anapenta mapiri a mtundu wofiirira (purple).

Achimwene ake aja atamaliza kudya anapemphera limodzi ndi Larisa ku chipinda kwake. Ndipo nthawi ndi nthawi mtsikanayu anali kupempherera azakhali ake mwachinunu.

“Chonde Ambuye banja limeneli lisathe, chitanipo kanthu, ndikudziwa kuti palibe chokolakani inu, ndipo ndikudziwa kuti mukhoza kuwathandiza azakhali anga,” anapemphera motero Larisa.

Pa nthawi ya nkhomaliro, Mayi ake anamufunsa Larisa mmene amamvera.

“Ndili bwino-bwino, osadandaula mwakuti ndazolowera basi,” anayankha motero mtsikanayu.

Atamwanso madzi, anabwerera ku chipinda kwake. Apa anayambano kumva njala, ndipo samafuna kuti ayasedwe kuti asiye kusalaku. Adakali ku chipinda kwake, anapita pa makina a intaneti nayamba kufufua za dziko la England. Anali wokondwa ndi zonse zomwe anawerenga zokhudza dziko la England ndipo anakhumba atadzapita kudzikoli tsiku lina.

Nkhomaliro itadutsa, Larisa anapempheranso limodzi ndi achimwene ake, koma apa ndiye anayamba kumva njala kwambiri. Sizinali zapafupi koma ankadziwa kuti zitere.

“Ndikumva njala, koma ndipirirabe,” anawauza Bambo ake motero.

“Ukwanitsa ndithu,” anamulimbikitsa motero Bambowo.

Mtsikanayu anapempheranso mwachinunu kuti azakhali aja asinthe ganio lawo ndipo anapempha Mulungu kuti amuthandize mpaka atatsiriza kulasa kudyaku. Anamwanso kapu ina yamadzi.

Patapita kanthawi, Mayi ake anaganiza kuti Larisa amwe madzi otentha.

Mayiwa anati, “Ngati sudya chakudya uyamba kumva kuzizira.”

Madzi otenthawa anamuchititsa Larisa kumva kufunda, ndipo iye anaganiza kuti asalingarirenso za chakudya, kenako anawapempheranso azakhali aja.

Pa nthawi ya chakudya cha madzulo, mtsikanayu anapita ku chipinda kwake, anapinda zovala zake zina, kupukuta desiki yake, naika zinthu zake zonse m’malo mwake.

Pa mapemphero a madzulo, banjali linasonkhana napempherera azakhali aja komanso linakambirana za m’mene tsikulo linayendera.

“Kodi Larisa, lero chimene chinakusangalatsa ndi chiyani?” Bambo ake anamufunsa.

Iye anayankha kuti, “Ndasangalala kuti ndidakalibe wamoyo.”

M’mawa wotsatira, mtsikanayu anadya nkhaka, karoti, ndi masamba mwamtima bi. Zokudyazi zinali zokoma zedi.

Patapita masiku angapo, pa nthawi ya mapemphero a banja lonse, Bambo anadziwitsa onse kuti azakhali amawapempherera aja asintha ganizo lawo lofuna kulekana ndi amuna awo.

Larisa anali wokondwa kuti atasala kudya Mulungu anayankha mapemphero ake.

Kodi pali chinthu chapaderadera chimene mukufuna Yehova akuchitireni lero lino?

Monga adachitira Larisa, mwinatu nanunso muyenera kusala kudya ndi kupemphera.

Kapenatu simukuyenera kusadya kwa tsiku lonse, kodi mukudziwa kuti pali njira zambiri zosalira kudya?

Kodi ndi zinthu ziti zomwe mukhoza kuzisiya kaye kwa tsiku lonse, kapena kwa maora angapo osazichita, kwinaku mukupemphera kuti Mulungu sakuchitireni chozizwa chapaderadera?

[Funsani maganizokuchokera kwa ana.]

Kusala kudya kwina ndikoti mukhoza osadya ma bisiketi, keke, ayisikilimu, ndi tizokudya tina tomwe mumadya musanadye chakudya cholimba, m'malo mwake mukhoza kumangodya zipatso ndi zamasamba.

Kapena mukhoza osacheza pa intaneti, monga patsamba la mchezo la Facebook kapenanso osaonera mafilimu kwa tsiku lonse.

Musaiwale kuti, tikasala chakudya, sizitanthauza kuti timakhala tikuganiza kuti tingathe kupeza madalitso a Mulungu. Monga adanenera munthu, iye adati, “Timasala chakudya pofuna kusachita zamdziko ncholinga choti tikhale ndi nthawi yokondwera ndi Yesu.”

Mukamasala kudya, onetsetsani kuti muli ndi nthawi yochulukira yoyankhulana ndi Khistu kupyolera m'pemphero. Nthawi zonse Yehova amamva mapemphero athu ndipo lye amakonda ana okonda kupemphera!

--Mathero a Nthano ya Ana--

Ulaliki

“Kukhala ndi Khalidwe Labwino mu Dziko Loipa”

[Komanso Pempho Loti Tisenze Mtanda]

Mlaliki: Melody Mason

Mawu Otsogolera

M'chaka cha 1994, mdziko la Rwanda munachitika chinthu choopsa ndi chochititsa mantha kwambiri, anthu opitirira 1 miliyoni anaphedwa. Mwa anthuwa, pafupifupi anthu 100,000 anali ziwalo za Mpingo wa Seventh-day Adventist.

Pa nthawiyi, anthu a mtundu wina amafuna kupheratu anzawo a mtundu wina. Anthu amene amachitiridwa ntopolawu amathawira ku matchalitchi kuti akapeze chitetezo poganiza kuti akabisala m'tchalitchi ndiye kuti saphedwa. M'tchalitchi china momwe anthuwa amathawira, gulu la ma Adventist linasonkhana pamodzi.

Zitseko za tchalitchichi zinali zitatsekedwa, ndipo aliyense anakumbatira mnzake, kwinaku akupemphera kuti Mulungu awateteze. Mosakhalitsa gulu la anthu onyamula zikwanje linafika nathyola chitseko chija, napha aliyense amene anawayandikira kuphatikizapo mbusa wa Mpingo wa Seventh-day Adventist. Zinali zoopsa kwambiri. Anthu ochepa okha ndi omwe anakwanitsa kuthawa.

Patapita masiku angapo, achiwembu aja atachoka, anthu omwe anakwanitsa kuthawa aja anabwera kuti adzatenge mitembo ya anthu amene anaphedwa kuti akaike. Mitemboyi imayenera kuikidwa mu dzenje, limodzi lalikulu. Anthuwa ali mkati monyamula mitemboyi, zinapezeka kuti m'modzi mwa anthu ochitiridwa chiwembuwa mtima wake unali ukugundabe, anali mayi Marie, mkazi wa mbusa wa Seventh-day Adventist yemwe anaphedwa uja. Mwansanga anathamangira nawo ku chipatala kuti apulumutse moyo wawo, imfa inali nawo pafupi mayiwa, koma mwachisomo cha Mulungu anapulumuka. Kwa zaka zitatu zotsatira mayiyu amati kugonekedwa m'chipatala natuluka. Kenako anayamba kukonzanso moyo wake.

Imfa ya mwamuna wa Mlongo Marie inali yopweteka, koma sanafune kubwezera m'malo mwake anaganiza kuti asakhale ndi khwidzi komanso udani koma akhululukire iwo onse omwe anachita izi.

Kukhululukira

UMBONI WA MLONGO MARIE

Mlongo Marie anawerenga m'bukhu la Aroma 12:20 kuti, "Koma ngati mdani wako akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu ummwetse; pakuti palutero udzaunjika makala a moto pamutu pake."

Dzina loti Marie si dzina leni-leni la mlongoyu

Mlongo Marie atazindikira kuti ena mwa anthu omwe anapha mwamuna wawo anagwidwa ndipo anali mndende yoyandikana ndi komwe amakhala, Mlongo Marie anapita kukawaona anthuwa nawanyamuliranso chokudya. Mu kupita kwa nthawi, iwo anasanduka "mayi" wa andendewa, amamukonda ndipo amabweretsa chokudya komanso mabulangete kwa andendewa. Pambali pa izi iwo anayamba kuphunzitsa omangidwawa Baibulo.

Tsiku lina akutumukira ku ndendeyi, mnyamata wina wotchedwa Rukundo anabwera kwa a Marie nagwada pamapazi a Mlongoyu nawapsopsona mapaziwo. Mnyamatayu anafunsa, “Amayi, mwandikumbukira?” Mlongo Marie anamuzindikira mnyamatayu kuti ndi yemwe anapha mwamuna wawo, zinawapweteka kwambiri. Sanangopha mwamuna wawo chabe koma ankafunanso kuwapha iwo.

“Amayi, mundikhululukira?” Anafunsa motero mnyamatayu misozi italenga mmaso mwake.

Kenaka mayiwa anamudzutsa Rukundo namukumbatira. “Ndinakukhululukira kalekale ndipo ndinaganiza zoti ndisakhale ndi nkhwidzi kapena udani mu mtima mwanga. Sindikufuna ndikhale moyo wa udani kapena wowawidwa mtima.

Kwa miyezi isanu ndi umodzi yotsatira Mlongo Marie amaphunzira Baibulo limodzi ndi Rukundo. Kutsatira izi, mnyamatayu anapanga chisankho choti abatizidwe. Pa tsiku lake lobatizidwa, Rukundo anaimilira pamaso pa anthu onse ku ndendeyi naulula machimo ake. Zinali zochititsa chidwi, nawo a Marie anali komwekonso kuchitira umboni.

Patapita zaka zingapo zochepe, boma la Rwanda linamukhululukira Rukundo, ndipo anatulutsidwa m’ndende. Makolo ake a Rukundo kuphatikizira abale ake nawo anaphedwa nawo limodzi ndi anthu 1 miliyoni anaphedwa aja, motero iye analibe kopita. Atatulutsidwa, lye analunjika kunyumba ya Mlongo Marie, anagogoda pa chitseko cha Mlongoyu. “Ndili ndekha-ndekha ndipo sindikudziwa kuti ndipita kuti. Nditani?” anafunsa motero. Akumwetulira, Mlongo Marie anati, “Inenso ndili ndekha-ndekha! Ndikutenga kukhala monga mwana wanga, ndipo pamodzi tizilindira kubwera kwa Yesu ndi kudzaonana ndi okonedwa athu.”

M’bukhu la *Christ Object Lessons*, alembamo kuti, “Kuunika ndi uthenga wotsiriza wachifundo woti uperekedwe kudziko, ndipo ndi vumbulutso la khalidwe la Mulungu la chikondi. Ana a Mulungu ayenera kuonetsera ulemerero Wake. M’makhalidwe komanso m’moyo wawo, iwo ayenera kuonetsera zimene chisomo cha Yehova chawachitira iwo.”

Mwinatu zochita za Mlongo Marie zikuoneka ngati zikuchitika mopyola muyezo poonetsera chikondi cha Yesu, ngakhale zikuoneka motere, ndikukhulupirira kuti ichi ndicho Chikristu chimene Yehova akutipempha kuti chikhale mwa ife. Nzovuta kuziganizira! Nzochitika mopyola muyezo! Ndipo nzovuta kuti munthu nkuzichita, kupatula munthu yekhayo yemwe ndi wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

Mmawa uno tiwerenga kuchokera pa 2 Petro 1:3-4. Tiyeni tiwerengenso mavesiwa.

“Popeza mphamvu ya umulungu wake idatipatsa ife zonse za pamoyondi chipembedzo, mwa chidziwitso cha lye amene adatiitana ife ndi **ulemerero ndi ukoma** wake wa lye yekha; mwa izi

adatipatsa malonjezano a mtengo wake ndi akulu ndithu; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nawo umulungu wake, mutapulumuka ku chivundi chili pa dziko lapansi m'chilakolako.”

Kodi zikuthanzu akati kuitanidwa ku ulemerero ndi ukoma? Ndikukhulupirira kuti zikuthanzu kukhala ndi khalidwe labwino mu dziko loipa. Zikuthanzu kukhala moyo woonetsera zimene chikondi cha Mulungu chinachita kwa ife.

Kukhala Moyo wa Chikristu Wosiyana ndi wa Dziko

CHITSANZO CHA YESU KWA OPHUNZIRA AKE

Timaphunzira kupyolera mu Uthenga Wabwino kuti Yesu akupereka kwa omtsatira Ake chitsanzo choti atsanze monga iwo ophunzira Ake chomwe nchosiyana ndi zochitika za dziko.

M'munsimu muli zitsanzo zoti tigawane:

- **Dziko limati** ngati ukufuna kupambana, nthawi zonse uyesetse kukhala patsogolo **pomwe Yesu akuti** mu ufumu Wake oyamba adzakhala omarizira (*werengani Mateyu 20:16*).
- **Dziko limati** dzithangate wekha ndi kupeza zosowa za iwe mwini **pomwe Yesu akuti** tiyenera kutumikira zosowa za anthu ena (*werengani Mateyu 20:28*).
- **Dziko limati** kondwera ndi kusangala ndi moyo wako m'mene ungathere **pomwe Yesu akuti** tidzikane tokha, tileke kuchita zinthu zamanyado mmalo mwakae tithandize ena (*werengani Mateyu 16:24*).
- **Dziko limati** chita zabwino ncholinga choti anthu akuone ndikukutama **pomwe Yesu akuti** ngati cholinga chathu ndi kuchita zabwino kuti anthu atione, kumwamba kulibe malo athu. Iye akutiiza mwatchutthu kuti, zabwino zomwe tichita m'tseri posafuna kuti ena atione ndi zomwe zimatengedwa monga khalidwe labwino (*werengani Mateyu 6:1, 6*).
- **Dziko limati** tikhale paubwenzi ndi anthu achuma komanso otchuka zathu ziyende **pomwe Yesu akuti** tiphunzire kutumikira ang'onong'ono awa, pakuti iwo ndi opambana mu ufumu Wake (*werengani Mateyu 25:45*).
- **Dziko limati** tidzikundikire chuma pakadali pano, ndipo tiyesetse kupeza chambiri m'mene tingathere **koma Yesu akuti**, chuma chomwe tikudzikundikira panochi chidzachita dzimbiri ndi kuonongeka. Chuma chokhacho chomwe ndi chokhalitsa ndi chomwe timagawana ndi ena (*werengani Mateyu 6:19, 20*).

Ngati tikuganiza kuti izi nzovuta, ndiyetu kulamula komwe kukubwera kutsogoloku nde eeee tikuyesa ngati nkopyola muyezo. Chikristu cheni-cheni chimaonetsera ulemerero wa Mulungu.

- **Dziko limati**, “diso kulipa diso” komanso “konda mnansi wako, dana ndi mdani wako,” **pomwe Yesu akuti**, kondani adani anu. Munthu akakupandani tsaya lamanja, mumtembenezire linalo (*werengani Mateyu 5:38-44*).

Tiyeni tione mwachidwi kulamula kuli m’munsi kuchokera m’bukhu la Luka.

Dalitsani iwo akutemberera inu, pemphererani iwo akuchitira inu chipongwe. Iye amene akupanda iwe pa tsaya limodzi umpatsenso linzake; ndi iye amene alanda chofunda chako, usamkanize malaya ako. Munthu aliyense akakupempha kanthu, umpatse; ndi iye amene alanda zako usazipemphanso. Ndipo monga mufuna kuti anthu adzakuchitirani inu, muwachitire iwo motero inu momwe. Ndipo ngati muwakonda iwo akukondana ndinu, mudzalandira chiyamiko chotani? Pakuti ochimwa omwe akonda iwo akukondana nawo. Ndipo ngati muwachitira zabwino iwo amene akuchitirani inu zabwino, mudzalandira chiyamiko chotani? Pakuti anthu ochimwa omwe amachita chomwecho. Ndipo ngati mukongoletsa kanthu kwa iwo amene muyembekeza kulandiranso, mudzalandira chiyamiko chotani? Pakuti inde anthu ochimwa amakongoletsa kwa ochimwa anzawo kuti alandirensomomwemo. Koma takondanani nawo adani anu, ndi kuwachitira zabwino, ndipo kongoletsani osayembekezera kanthu konse, ndipo mphototho yanu idzakhala yaikulu, ndipo inu mudzakhala ana a Wamkulukuluyo; chifukwa iye achitira zokoma anthu osayamika ndi oipa. Khalani inu achifundo monga Atate wanu ali wachifundo. Ndipo musamaweruzana, simudzaweruzidwa (Luka 6:28-36).

Tangoganizani kuti posachedwapa ntchito yolalika uthenga itsirizika ndipo Yesu adzatitenga kunka kwathu, ngati tinatsanza chikondi cha Khristu. Iye akuti, “Mwa ichi adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondano cha wina ndi mnzake” (*Yohane 13:35*).

Ngakhale zili choncho, ife sititsatira zomwe wanena Khristu-zi. Ndipo ndi zovuta kukamba za kukonda adani athu monga wanenera Yesu pamene tikulephera ngakhale kukonda anzathu komanso ziwalo zina za mpingo motere. Tikusoweka Mzimu Woyera kuti akhazikike mkati mwathu, pakuti popanda Khristu, ife tili chabe.

Timapempherera mtendere wochuluka ndi chimwemwe, koma tiyenera kupemphera kuti Mulungu wa mtendere ndi chimwemwe akhazikike mwa ife kupyolera mwa Mzimu Wake (*Yohane 14:27, 15:11*). Timapemphera kuti tikhale okonda kwambiri, komatu tiyeneranso kupemphera kuti chikondi cha Yesu chikhale mwa ife (*Yohane 15:10*). Timapemphera kuti tikhale Akhristu abwino, koma tikuyenera kupemphera kuti Khristu Mwini akhale mwa ife kupyolera mwa Mzimu Woyera-monga Iye afunira (*Aefeso 2:22*).

Kutembenuza Tsaya Lina

UMBONI WA A TOM

Ndigawane nanu nkhani ina. Nkhaniyi ndi yokhudza mwamuna wina dzina lake Tom.

A Tom anali mphunzitsi wa Baibulo ndipo amatumikira ku dera lina lomwe kulalikirako uthenga wabwino sichinali chinthu chapafupi mwakuti Akhristu ambiri amaphedwa kumeneko.

A Tom ndi akazi awo anachita ngozi atakwera njinga yawo yamoto. Ngoziyi inachitika pamene awiriwa anaimitsidwa pambali pa mseu ndipo wanjinga yamoto wina anawagunda. Mwayiwo, palibe yemwe anavulala modetsa nkhwawa, ngakhale kuti njinga ziwiri zonse zinaphwanyika. Munthu yemwe anawagundayu anali ataledzera, ndipo anali mfumu ya mudzi wina woyandikira.

A Tom sanakwiye chifukwa cha ngozi ija, m'malo mwake anawafunsa amfumu aja kuti, "Tsono titani pamenepa?" Bambo Tom anafunsa motero.

"Mukuyenera mundikonzetsere njinga yanga!" anayankha mwa mwano chotere amfumuwo.

Posafuna kukangana, ngakhale analibe ndalama zochulukana, a Tom anapereka ndalama zokonzetsera njingayo. Komatu sanalekele pomwepa. Iwo anakayendera amfumu aja ndipo anayamba kufunafuna njira zowathandiza pamodzi ndi banja lawo, Bambo Tom anadziperereka kuti akawalimira amfumuwo m'munda mwawo. Iwo anawachitira amfumu pamodzi ndi banja lawo zinthu zabwino mwakuti anthu a m'mudzi umenewo anali kuona zonsezi.

Tsiku lina munthu wina anawafunsa a Tom kuti, "Mfumu yathu ndi yamwano. N'chifukwa ninji mukuwachitira zabwino? Palibetu yemwe amakhala bwenzi la amfumuwa!"

"N'chifukwa choti ndimamukonda Yesu ndipo ndikufuna kugawana chikondi Chake ndi ena," anayankha motero a Tom.

Mosakhalitsa anthu ena a m'mudziwo anawapempha a Tom kuti awaphunzitse zambiri zokhudza Yesu. Sipanatenge nthawi, Bambo Tom anayamba kuwaphunzitsa anthuwa Baibulo, mwakuti ena anabatizidwa. Chodabwitsa chachikulu nchakuti mudzi umenewo m'mbuyomo a Tom anayesera kukalalikirako uthenga wabwino koma sizinawayendere. Koma tsopano chifukwa cha kukoma mtima komwe anaonetsera amfumu a m'mudzimu, Mulungu anachipanga kukhala chotheka kuti iwo (a Tom) akagawane ndi ena za Yesu.

Tangoganizani-anakati a Tom anayankhula mosakhala bwino itachitika ngozi ija monga achitira anthu ambiri, iwotu sakanafalitsa uthenga wa Khristu m'mudzimu. Kodi mungathe kulingarira za momwe zinthu zingakhalire zosiyana mdziko komanso mu mpingo wathu lero lino, ngati titachita zinthu mosiyana pothandizana wina ndi mnzake mosadzikweza, ngakhale pamene talakwiridwa?

Tom si dzina lawo leni-leni

M’bukhu la *Ministry of Healing* munalembedwa mawu awa,

“Sitikuyenera kulola cholakwika chilichonse chomwe chinachitika kapena choganiziridwa kuchita ulamuliro pa ife. Kunyada ndi mdani amene tiyenera kumuopa koposa. . . . Palibe chipambano china choposa kugonjetsa kunyada. Tisalole zilakolako zathu kutitsogolera ku zoipa. Sitikuyenera kutaya nthawi ndi kufuna kukwaniritsa zokhumba zathu, koma tiyenera kukangalika ndi kupulumutsa miyoyo.”

Kumbukirani kuti,

“Yehova akhoza kuchita zinthu zambiri mu ora limodzi kuposa zomwe ife tingachite moyo wathu wonse, ndipo pamene Iye waona kuti anthu Ake ndi odzipereka, ndikukutsimikizirani, zazikulu zidzachitika mu kanthawi kochepe, ndipo uthenga wa choonadi udzafikira mbali zina zadziko komwe unali usanafikeko ndi kale lonse.”

Kukhala ndi Khalidwe Labwino mu Dziko Loipa

Malingana ndi Malembo, aliyense wa ife watumidwa, kupatulidwa, ndi kupatsidwa mphamvu kuti agwire ntchito yopatulika-yomwe ndi kugawana ndi dziko lapansi loonengekali chikondi cha Mulungu. N’cholinga choti izi zitheke, tiyenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi kukhala ndi khalidwe labwino, loyenera, ndi losasintha pamene tatumidwa kugwira ntchito yopatulikayi. Zilibe kanthu kuti anthu akutichitira zotani, komanso zikoka zomwe zatizungulira. Tikupemphedwa kuti tikhale okhulupirika, “opanda chilema pakati pa mbadwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko a m’dziko lapansi” (*Afilipi 2:15*).

“Ulemerero wa Mulungu ndiwo umapereka khalidwe labwino kwa ana Ake,” anatero Mlongo Ellen White.

Kodi khalidwe labwinoli ndi lotani kweni-kweni? Limakhala lotsanza Yesu! Yesu anali chipatso cha Mzimu pamene Iye anali mu thupi la munthu!

Pa Agalatiya 5:22 ndi 23 timapezapo nkhani iyi yoti “Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso...”

Mwaonatu tsopano, Mzimu wa Mulungu akakhala mwa ife, chipatso cha Mzimu Woyera chidzaonekera. Osati chimodzi chokha ayi, *koma zonse!*

Kupholera m'moyo Wake, Yesu anaonetsera chitsanzo cha m'mene tingakhalire anthu a khalidwe labwino ngakhale tili m'dziko loipa.

Mlongo Ellen White analemba mawu awa,

“Moyo wa Khristu waonetsa zimene munthu angachite pokhala oyanjana naye mu umulungu Wake. Zonse zomwe Khristu analandira kuchokera kwa Atate nafenso tikhoza kulandira. Tsonotu pemphani ndipo mulandira. Ndi chikhulupiriro chosafoka monga cha Yakobo, komanso ndi kulimbika mtima monga Eliya, pemphani zonse zomwe Mulungu analonjeza.”

Ili likhale pemphero lathu tsiku ndi tsiku! Mulungu watilonjeza kutipatsa zochuluka, n'chifukwa ninji tikufuna zochepa?

Kumbukirani, kuti iyi si nkondo ya kuthekera kolamulira maganizo kapena kudziletsa kwakukulu. Iyi ndi nkondo ya mtima. Kodi mtima wathu taupereka kwa yani?

Tsoka ilo, dziko latiphunzitsa kuti moyo wathu wagonera pakuyesetsa kuti tikhale patsogolo-kuganiza zathu zokha, kudzikonda! Kukonda zinthu zomwe zimatipanga kukhala okhutitsidwa ndi okondwa timazona kukhala zoyenera kwa ife, anthu amatero. Komatu malingana ndi Malembo uku nkuganiza koopsa!

Zomwe mitima yathu imafuna nthawi zambiri sizikhala zolungama kapena zolondola. “Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosachiritsika, ndani angathe kuudziwa?” akudandaula motero mneneri Yeremiya (*Yeremiya 17:9*). Sitingakhale ndi moyo wabwino ngati tili odzikonda komanso tikutsatira mtima wathu!

Nthawi zonse tiyenera kumapemphera, *“Ambuye, tengani mtima wanga! Usintheni! Ndipo mundipange kufanana ndi Inu.”*

“Nkhondo yolimbana ndi kunyada ndi nkondo yaikulu imene inachitikapo [kapena imene ichitike]. Kugonjera ku makhalidwe onyada, kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu, ndi nkondo ndithu; koma mtima uyenera kuperekedwa kwa Mulungu kuti lye aupange kukhala watsopano ndi kuuyeretsa.

Pempho Loti Tinyamule Mtanda

Mu Luka 9:23, 24 Baibulo likutiya kuti, “Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wake tsiku ndi tsiku, nanditsate Ine. Pakuti amene aliyense akafuna

kupulumutsa moyo wake, iye adzautaya, koma amene aliyense akataya moyo wake chifukwa cha Ine, iye adzaupulumutsa uwu.”

Kwa munthu yemwe wangoimva koyamba nkhani yokhudza kunyamula mtanda, chikhoza kuoneka chinthu chopanda chikoka. Ngakhale zili chomwechi, motsutsana ndi ganizo lodziwika, tchutchutchu wosangalatsa ndi wakuti tikanyamula mtanda wathu, zimachititsa kuti Mulungu atichotsere m’moyo mwathu zinthu zopinga zomwe zingatilepheretse ulendo wopita kumwamba. Tsono, zinthu zimene dziko lingazione kukhala zopweteka kwa ife ndi zotipangitsa kukalowa kumwamba.

Mulungu sakutipempha kuti tipereke nsembe yeniyeni kwa Iye. Mu zinthu zambiri Iye akutipempha ife kuti timugonjere, komatu potero timakhala kuti tikutaya zinthu zomwe zingatilepheretse ulendo wopita kumwamba. Ngakhale pamene tikupemphedwa kuti tisiye zinthu zomwe nzooneka zabwino, tikhoza kukhala otsimikizika kuti Mulungu akutikonzera chinthu china chopambana.

Nkutheka muli pankhondo yolimbana ndi tchimo lina lobisika kapena mphamvu ina yauzimu m’moyo mwanu imene mukulephera kuigonjetsa. Munthu wina wanzeru adati, “Nkhani yaikulu si yokhudza chidwi chimene mwaika pa nkondo yolimbana ndi tchimo ayi-koma m’mene inu mwadziperekerwa kwa Mulungu.”

Tiyeni tisaiwale kuti wokhulupirika akasiya tchimo ndi kudzipereka kwa Mulungu, sizikutanthauza kuti munthuyu ndi wolephera ayi, iye ndi “mogonjetsi kupyolera mwa Yesu!”

Tikadzipereka kwa Khristu ndi kunyamula mtanda Wake, chinthu chodabwitsa chimachitika. M’malo moti mtandawu ukhale wolemera, tizazindikira kuti “Pamene tanyamula mtanda, mtandawo umatinyamula ife.” Tiyenera kupereka mphamvu zathu kwa Yesu ndi kulola mphamvu Yake ichotse kulemera kwa mtanda. Mphamvu yathu ndi yolefuka ndipo singachite kanthu. Nthawi yomwe talola Khristu kutenga ulamuliro wa mtima wathu, Iye amatipatsa ife chigonjetso.

“Pamene mwadzipereka kwathunthu kwa Mulungu, pamene mwadzimva kukhala operewera pamaso pa Yesu, mudzapatsidwa chigonjetso chomwe chidzakhale chimwemwe chimene simunachiganizirepo nkale lonse.”

Mlongo Ellen White akulongosola motere: “Pamene mukumva kukhala woperewera pamaso pa Yesu....” Pamene tagonja pamaso Pake, kodi zimenezi zikutanthauza chani?

Dothi la Mtengo Wapatali

Kuumva mtima kukhala wosweka ndithudi ndi kudzipereka kosangalatsa kwambiri komanso nsembe yopatulika yomwe tingapereke kwa Mulungu. Indedi, ndi nsembe yokhayo imene

tiyenera kupereka. Baibulo limatiuza kuti, “Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka; Inu, Mulungu, simudzaupeputsa mtima wosweka ndi wolapa” (*Masalmo 51:17*).

Tanthauzo la liwu loti “wolapa” mu Salmo 51:17 likuchokera ku liwu la Chihebri loti *dâkâh*, lomwe limatanthauza kuti: *kung’ambika, kupuntha nakhala tizidutswa, kuswa, kusinja, kusasa, kapena tingoti kufafaniziratu.*

Taganizirani za izi! Ngati chinthu chasweka pang’ono, mukhoza kuchimata, koma simungathe kumata chinthu chimene chasweka ndipo chasanduka dothi. Ifetu tili chimodzimidzi-ndife dothi...osweka.... zotengera zosweka!

Mlongo Ellen White akuti: “Mwayi waukulu motani nanga kwa ife amene tili mu thupi lomwe limafa, kuti ndife dothi ndi phulusa, ndipo Khristu akutikonzanso kuti tiyanjane ndi Yehova.”

Tikaganiza, sikuti timangokhala pamaso pa Mulungu kokha, koma dothi ndi limene Iye amagwiritsa ntchito mobwereza-bwereza kuti achite zozizwa Zake.

Pachiyambi, Mulungu anabzala mitengo ndi zomera m’fumbi, M’manda wa Edene nazipangitsa izo kukula ndi kubereka chipatso (*Genesis 1:1*). Kenako Yehova anapanga mwamuna ndi mkazi, pachimake pa ntchito yolenga, anthuwa anawapanga kuchokera ku dothi nawalamula iwo kuti abalane ndi kuchulukana (*Genesis 2:7, 1:28*).

Taimani kwa kanthawi kochepe. Kodi timazindikira kuti zonse zomwe timachita ndi kupeza, machitachita athu onse abwino, kupatula mpweya wopereka moyo, mwazi wa Yesu, ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, ndi zopanda pake kuposa dothi? Chikhalirecho, nthawi zambiri timadzitukumula kwambiri ndi kudzitamandira!

Mwamwayi, ngakhale themberero la tchimo linadza padziko lapansi, Yesu anali wokhudzika ndi munthu (dothi). Iye anabwera padziko lapansi kudzapitiriza ntchito Yake pakati pa fumbi la anthu (*1 Samueli 2:8*). Pamene Khristu anagwiritsa ntchito dothi kuti wakhungu uja aone (*Yohane 9:5-6*), ndi dothi komanso kusweka kwa moyo zimene Iye kawiri-kawiri akugwiritsa ntchito lero lino kuti abwezeretse kwa ife maso auzimu. Iyetu ndi katswiri posakaniza madzi ndi dothi pofuna kupanga dongo. Ndi pokha-pokha pamene tili dothi loti likhoza kuumbidwa taumbidwa ndi Woumba Mbiya Waluso Kwambiri pamene timasanduka kukhala munthu amene Iye amafuna pamene ankatilenga (*Yeremiya 18:6*).

Monga adalembera wolemba wina mochititsa chidwi kwambiri, “Dothi silisonyeza mapeto a zonse. Dothi liyenera kutizindikiritsa kuti kuli moyo wina watsopano ukatha uno.”

Ndithudi, dothi likhoza kusanduka lokongola ngati lili m’manja mwa Mulungu wachikondi. Ndipo dothi lomwe ladzipereka kwa Yehova ndi la mtengo wapatali! Pothirira ndemanga pa izi, tikuuzudwa kuti,

“Palibe chinthu chimene Satana amachiopa kwambiri koposa kuti anthu a Mulungu akonze njira yawo pochotsa cholepheretsa chilichonse, ncholinga choti Ambuye atsanulire Mzimu Wake ku mpingo womwe ukusautsika. . . .Mvula masika idzadzaza, ndipo madalitso a Mulungu adzadzadzaza mwa munthu aliyense amene mtima wake wayeretsedwa ku chonyansa chilichonse.”

Pokhala inu dothi, kodi mwadzipereka kwa Yesu? Kodi mwamutulira lye zofooka, machimo, ndi kusweka mtima kwanu? Tikachita izi, lye adzachita zozizwa ndi dothi limeneli.

Kudandaulira

Mnzanga, lero lino, Yesu akukuonetsa dzanja Lake cha zipsera za mabala a misomali ndipo akuti, “Ndipatse dothi lako.” Kuitanira kopambana nanga! Tiyeni timupatse dothi lathuli-dothi la mtima wosweka ndi woperewera, mtima umene ukuti, “Ambuye, indedi ndikufuna kuyenda Nanu. Ndikufuna mundisithe mu chifanizo Chanu, kuti ndithe kukonda ena ndi chikondi chomwe mwandipatsa. Ndikufuna kukhala Mkhristu wa khalidwe labwino monga mwandiitana kuti ndikhale wotero. Koma ndilibe china chokupatsani kupatula kulakwa ndi kusweka kwanga. Ndipereka kwa Inu zofooka zanga, zowawa, kuwawidwa mtima, ndi misozi yanga. Machitachita anga amene ndimawayesa abwino, ndi opanda pake pamaso panu ndipo ndi dothi, koma ndili wokonzeka kupereka dothi langa lonse kwa Inu, ndi kukhala dongo mu dzanja Lanu monga Inu Woumba Mbiya Waluso. Tengani ulamuliro wa mtima wanga Ambuye! Chilichonse chomwe munene, ine ndimvera.”

Ngati ili lilinso pemphero lanu lero lino, kodi mungaimene nane pamodzi, pamene pemphero lotsiriza likuperekedwa?

--Mapeto a Ulaliki--

Cholengeza: Mubwere masanawu ku chilinganizo chatu chomwe mutu wake ndi “Mtima Umene Mulungu Amakondwera Kukhalamo.”

Sabata Skulu

Kutsekula Zitseko za Nyumba Yosungiramo Mphamvu Kumwamba

[Mfundo za Baibulo Khumi ndi Ziwiri Zofunikira mu Kupembedzera]

Wolemba: Melody Mason

Mndandanda wa Chilinganizo umene Tauyerekeza (Mukhoza Kuusintha)

Nyimbo Yoyamba: Sankhani nyimbo kuchokera mu Khristu mu Nyimbo

Pemphero Loyamba

Kulandira anthu ndi alendo

Mawu Otsogolera

Nyimbo Yapadera

Vesi Lotsogolera: Yakobo 5:16

“Chifukwa chake muvomerezane wina ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m’machitidwe ake.”

Mutu wa Chilinganizo: “Kutsekula Zitseko za Nyumba Yosungiramo Mphamvu Kumwamba”

Umboni wa Kuyankhidwa kwa Pemphero: Mukhoza kuchita kapena ayi

Nyimbo Yotsiriza: 211-“Madalitso Ngati Mvula” (Khristu mu Nyimbo)

Pemphero Lotsiriza

Mapemphero Amayi Padziko Lonse Lapansi

M’chaka cha 1990, nthambi ya Utumiki wa Amayi ku likulu la Mpingo wa Seventh-day Adventist linakhazikitsa Tsiku la Mapemphero Amayi Padziko Lonse Lapansi. Ili ndi tsiku lapadera-dera

limene limachitika Lasabata loyambirira la mwezi wa March chaka chilichonse. Patsikuli amayi onse padziko lapansi amalumikizana mu pemphero.

Sabata Skulu

Mukhoza kuchita yaifupi kapena yaitali poonjezerapo maumboni mwa kufuna kwanu!

Kutsekula Zitseko za Nyumba Yosungiramo Mphamvu Kumwamba

[Zinsinsi za Baibulo Khumi ndi Ziwiri Zofunikira pa Kupembedzera]

Wolemba: Melody Mason

Kodi zimakuchitikirani kuti mwapemphera kwambiri koma simukuyankhidwa? Zoona zake ndi zoti, pamene mukupemphera kwambiri, ndi pomwenso zimaoneka kuti zinthu zikusokonekera. [Perekani chitsanzo cha zomwe zinakuchitikirani kapena chitsanzo china choonetsera]

Ngakhale kuti Mulungu amatikonda ndipo amafuna kuyankha mapemphero athu, chokondweretsa kwambiri pa zimene timapempha kapena kuganiza, pali ndondomeko zina zimene tiyenera kukwaniritsa kuti tilandire madalitso Ake odzadza.

M'bukhu la *Christ's Object Lessons*, Mlongo Ellen White akuti,

Malonjezano a Mulungu ali ndi dongosolo la pangano ncholinga choti akwaniritsidwe, ndipo pemphero silisinthira izi. . . Anthu amene amatula nkhwawa zawo kwa Mulungu, kufunafuna madalitso a Mulungu koma osakwaniritsa dongosolo la pangano Lake, amakhala kuti akunyoza Yehova. Iwo amavomereza kuti ndi Khristu amene angakwaniritse malonjezo amene analonjezedwa, koma anthuwa sachita zinthu zimene zimaonetsera chikhulupiriro mwa Khristu ndi chikondi chawo pa Iye.

Kodi Mulungu amafuna tichite dongosolo lotani? “Iye amanena momvekeratu kuti kupempha kwathu kukhale molingana ndi chifuniro cha Iye; tiyenera kupempha zinthu zomwe Iye watilonjeza, ndipo tikalandira tizigwiritse ntchito mu chifuniro Chake. Tikachita zomwe Iye akufuna, tidzakhala otsimikizika kuti mapemphero athu adzayankhidwa.”

Tikawerenga Baibulo, tipeza dongosolo la kachitidwe ka zinthu kosasintha. Chidwi cha Mulungu chili pa miyoyo ya anthu, ulemerero wa dzina Lake, komanso kukhazikitsidwa ndi kumangidwa kwa ufumu Wake. Iye ndi chikondi. Ichi ndicho chionetsero cha chifuniro cha Atate wathu. Tikapemphera malingana ndi chifuniro komanso ulemerero Wake-kuti ufumu Wake uthe kukhazikitsidwa-tikhoza kupemphera motsimikizika ndi molimba mtima, ngakhale anthu akuona kuti zomwe tikupemphererazo ndi zosatheka, chifukwa choti Yohane akutilimbikitsa kuti, “Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tili nako kwa Iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa chifuniro chake, atimvera” (1 Yohane 5:14).

Chinsinsi Cholandidira Madalitso a Kumwamba

Kupemphera ndi chinsinsi cholandidira madalitso a kumwamba. Nazi zinsinsi khumi ndi ziwiri za m'mene mapemphero athu ayenera kukhalira. Kupempherera malinga ndi chosowa cheni-cheni, ndi mtima woona, kupemphera malingana ndi chifuniro cha Mulungu, ndi kuuziridwa kwa Mzimu Woyera, mwa chikhulupiro, momvera ndi kulapa, ndi kukhululuka, ulemu, ndi kutumikira koono, kukoma mtima, kudziwa Iye amene amapatsa, ndi kulimbika mtima. Tsopano tiyeni tione mfundozi pazokha-pazokha.

Chinsinsi Choyamba: KUPEMPHERA MOLINGANA NDI CHOSOWA CHENI-CHENI

Tizipemphera malinga ndi chosowa cheni-cheni. Kodi mumadziwa kusoweka kwanu kwa Mulungu komanso chithandizo chimene Iye angapereke?

Pali dongosolo lina lapadera limene tiyenera kulitsata ncholinga choti Mulungu amve ndi kuyankha mapemphero athu. Chinthu chimodzi choyambirira nchakuti ife timamva kuti tikusoweka thandizo la Mulungu. Iye walonjeza, "Pakuti ndidzathira madzi pa dziko limene lilibe madzi, ndi mitsinje pa nthaka youma," Yesaya 44:3. Iwo amene amamva njala ndi ludzu lofuna kukhala olungama, komanso akufunafuna Mulungu, adzakhala ndi chitsimikizo choti adzapeza zosowa zawo.

Yehova sataya nthawi poyesetsa kuti akwaniritse zosowa za anthu amene akudzimva kukhala okwanira pawokha. Iye akufuna zotengera zopanda kanthu.

Chinsinsi Chachiwiri: KUPEMPHERA NDI MTIMA WOONA

Tiyenera kupemphera ndi mtima woona. Mlango Ellen White akutiululira kuti,

Pemphero lililonse loona limamvedwa kumwamba. Likhoza kusapempheredwa bwino; koma ngati mtima wa munthu wopempherayo uli mu pempheroyo, ilo lidzakwera kupita mu kachisi wakumwamba m'mene Yesu akutumikira, ndipo Iye adzapereka zopempha zathu kwa Atate moyenerera, mosajejema, mwa ukoma ndi mokondwetsa pozinunkhiritsa izo ndi chiyero Chake.

Mosajejema! Nzokondweretsatu, si choncho?

Chinsinsi Chachitatu: KUPEMPHERA MU CHIFUNIRO CHA MULUNGU

Tizipemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Timafunsa kuti "kodi ndingachidziwe bwanji chifuniro Chakecho?" Kuti timvetsetse chifuniro cha Yehova, tiyenera kudziwa Mawu a Mulungu. Tikamvetsetsa Mawu, tidzamvetsetsa mwa mvemvemve chifuniro cha Yehova.

Chilichonse chomwe ndi chogwirizana ndi chilengedwe cha Mulungu chilinso molingana ndi chifuniro cha Iye. Sitikuyenera akukhala odadwa kuti Mulungu akufunitsitsa kutipatsa ufulu ku

uchimo, kutipatsa mphamvu zogonjetsera mdani, mtendere weni-weni, chimwemwe choposa, mphamvu yoti timtumikire, mabanja abwino, ndi kukhala opindula ku ufumu Wake. Izi ndi zinthu zimene Iye anazinena kupyolera m’Malembo kuti amakondwera kuzipereka.

Mapemphero athu akakhala molingana ndi cholinga cha Ufumu wa Mulungu, ndiye kuti tikhoza kupemphera motsimikizika. Ngati sitikudziwa chifuniro cha Mulungu, ndiye kuti tipemphe nzeru kwa Iye monga mmene Yakobo 1:5 akutiuzira.

Chinsinsi Chachinayi: KUPEMPHERA MOUZIRIDWA NDI MZIMU WOYERA.

Tiyenera kupemphera mouziridwa ndi Mzimu Woyera. Nthawi zina cholinga cha mapemphero athu si cholinga cha Yehova. Pamene tikupemphera, m’ malo moti tingogwada kenako nkuyamba nkumuza Mulungu zosowa zathu, tikuyenera kuyamba kaye tamufunsa Iye kuti kodi akufuna tipemphe chiyani, izi timazizindikira pamene tazama pakuwerenga Mawu a Mulungu.

Yehova akutilimbkitsa ife kuti, “Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe, ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikulu, ndi zolakika, zimene suzidziwa” (*Yeremiya 33:3*).

Mlongo Ellen White akutiululira kuti, “Ngati tisendeza chifupi ndi Mulungu, Iye adzasendeza chifupi nafe, ndipo ulemerero Wake udzatitsogolera. Adzasintha zopempha zathu, natiphunzitsa kupempha zinthu zokhazo zomwe Iye analonjeza kuti adzatipatsa.

Chinsinsi Chachisanu: KUPEMPHERA MWA CHIKHULUPIRIRO

Tikuyenera kupemphera mwa chikhulupiriro. Kodi timapemphera kwa Mulungu mwa chikhulupiriro? Yakobo 1:6, “Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi funde la Nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo.”

M’bukhu la *Steps to Christ* mwalembedwa kuti, “Pemphero ndi mfungulo zotsegulira zipinda za kumwamba, m’mene muli chuma chosefukira cha Wamphamvuzonse.”

Chinsinsi Chachisanu ndi Chimodzi: KUMVERA NDI KULAPA

Anthufe pamene tikupemphera tiyenera kukhala ndi mtima womvera ndi wolapa. Izi zikutanthauza kuti, pamene tikupempha kwa Mulungu kuti ayankhe mapemphero athu, ndiye kuti tikufunafunanso kuti timumvere Iye m’mene tingathere, ndi kuti atichotsere tchimo lililonse-osati chifukwa choti kumvera kwathu kumatipanga kukhala woyenera kulandira madalitso Ake, koma chifukwa choti kumvera kwathu ndi umboni woti timamukonda Iye.

Mlembi wa Masalmo, pa Masalmo 66:18, akuti, “Ndidakasekera zopanda pake m’mtima mwanga, Ambuye sakadamvera.”

Ichi n'chifukwa chake tikukumbutsidwa kuti, “Ngati timumvera Iye mochepe chabe, malonjezo Ake sadzakwaniritsidwa kwa ife.”

Pamene Sauli anaitanidwa kuti akhale mfumu ya Israyeli, anali wofatsa ndi womvera. Anali wololera kukonzedwa monga mtumiki wa Yehova ndipo amachita chilichonse chomwe Mulungu wamuuza kuti achite. Pachifukwa ichi, Mulungu anamudalitsa iye. Ngakhale zili chomwechi, atatchuka ndikukhala ndi ukadaulo, anayamba kunyada. Anayamba kuchita zinthu payekha osafunsira nzeru kwa Mulungu.

Yehova atalamula Sauli kuti awononge mtundu wonse wa Amaleki, Sauli sanamvere zonse zimene anauzidwa. Mfumuyi inasankha kupha anthu ena nasiyako ena ndi moyo, atafunsidwa anapereka zifukwa zosamveka. Zitachitika izi, chotsatira chomwe tikuuzidwa chokhudza Sauli ndi pamene iye akufunsira nzeru kwa Mulungu pa nkondo ya Israyeli ndi Afilisti. Komatu Mulungu anali ataleka kumva mapemphero a Sauli chifukwa choti Sauliyu anali osamvera komanso amapereka zifukwa zosamveka. Atazingwa, Sauli akufunsira nzeru kwa openduza. Mwatsoka, Afilisti apambananso nkondo ija kugonjetsa Aisrayeli. Sauli sikuti wangotaya moyo ndi ufumu wake kokha; iye watayanso mzimu wake (*werengani 1 Samueli 28:15-25, 31:1-13*).

Pemphero ndi lopanda pake ngati munthu wopempherayo sakhala moyo wolingana ndi pemphero. Mlongo Ellen White akutichenjeza kuti, “Moyo wathu ukhale molingana ndi mapemphero athu.” N'zosadabwitsa kuti mapemphero ambiri lero lino ndi ochepe mphamvu! Izi ndi chifukwa choti timakhala moyo wosemphana ndi mapemphero athu, tikukhala moyo wochimwa mbali ina tili ndi Mulungu. Tikuyenera kulira kwa Mulungu kuti asinthe mitima yathu ndi kutipulumutsa!

Chinsinsi Chachisanu ndi Chiwiri: KUPEMPHERA NDI MTIMA WOKHULULUKA

Tikuyenera kupemphera ndi mtima wokhululukira. Yesu akutilangiza kuti, “Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, khululukirani, ngati munthu wakulakwirani kanthu; kuti Atate wanunso ali Kumwamba akhululukire inu zolakwa zanu” (*Marko 11:25*).

Koma Khristu sakulekera pomwepo, pa Chiphunzitsa Chake cha Paphiri, Iye akuti, “Chifukwa chake ngati ulikupereka mtulo wako pa guwa la nsembe, ndipo pomwepo ukakumbukira kuti mbale wako ali ndi kanthu pa iwe, usiye pomwe mtulo wako kuguwako, nuchoke, nuyambe kuyanjana ndi mbale wako, ndipo pamenepo idza nupereke mtulo wako” (*Mateyu 5:23, 24*).

Kuuziridwa kukupitirirabe: “Pamene tadza kupempha chifundo ndi madalitso kwa Mulungu, m'mitima mwathu muyenera kukhala mzimu wachikondi ndi wokhululukira. . . Ngati tikuyembekezera kuti mapemphero athu ayankhidwe tikuyenera kukhululukira ena molingana ndi khumbo lathu loti ifenso tikhululukidwe.”

Chinsinsi Chachisanu ndi Chitatu: KUPEMPHERA MWAULEMU

Makhalidwe akhale olingana ndi pemphero ndi olemekeza banja lathu. 1 Petro 3:7 akulamula kuti, “Momwemonso amuna inu, khalani nawo monga mwa chidziwitso, ndi kuchitira mkazi ulemu, monga chotengera chochepa mphamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa chisomo cha moyo, kuti mapemphero anu angaletsedwe.”

Kodi sizodabwitsa kuti ngati timakonda kapena sitikonda apabanja pathu zimenezi zikhoza kulepheretsa kuti mapemphero athu asamayankhidwe?

Chinsinsi Chachisanu ndi Chinayi: KUPEMPHERA POTENGERA KUTI NDIFE ADINDO

Khalidwe lathu monga ife adindo okhulupirika likhalenso mu mapemphero athu. Kodi mukudziwa kuti ife monga “adindo” a zinthu za Mulungu zimakhudza mapemphero athu?

Mulungu monga wopereka madalitso, Iye amafuna kagawo kochepe pa chuma chathu. Gawoli ndi loti lithandizire kupititsa patsogolo ntchito yolalikira uthenga wabwino. Ndipo popereka gawoli kwa Yehova, timakhala kuti tikuthokoza kuti Iye amatipatsa mphatso Zake. Koma ngati tiumira posapereka zomwe ndi Zake, angatipatse bwanji madalitso Ake? . . . kodi tikuganiza kuti Iye angatipange kukhala adindo woyang’anira zinthu zakumwamba? N’kuthekatu kuti mavesi ali m’munsimu ndi yankho ku mapemphero osayankhidwa.

Yehova anatumiza uthenga Wake uwu kupyolera mwa mneneri Malaki:

“Kodi munthu adzalanda za Mulungu? ndipo inu mundilanda Ine. Koma mukuti, Takulandani zotani? Limodzi limodzi la magawo khumi, ndi zopereka. Mutembereredwa ndi temberero; pakuti mundilanda Ine, ndinu mtundu uwu wonse. Mubwere nalo limodzi limodzi lonse la khumi, ku nyumba yosungiramo, kuti m’nyumba mwanga mukhale chakudya; ndipo mundiyese nako tsono, ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi kukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira” (Malaki 3:8-10).

Chinsinsi Chakhumi: KUPEMPHERA NDI MTIMA WOPATSA

Monga ife opemphera, tiyenera kukhala ndi khalidwe lopatsa kwa osowa. Kukhala mdindo wabwino wa Chikhristu zimaposa pongobwezera chakhumi chathu. Zikuphatikiziranso kuthandiza osowa. “Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino, ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo” (*Yakobo 4:17*).

Palinso mfundo ina yomwe ndi yofunikira kwambiri kuti mapemphero athu aziyankhidwa. Tikuchenjedwa kuti, “Wotseka makutu ake polira waumphawi, Nayenso adzalira koma osamvedwa” (*Miyambo 21:13*).

Chinsinsi Chakhumi ndi Chimodzi: KUPEMPHERA KUTI TIMUDZIWE WOPATSAYO

Tiyenera kupemphera kuti timudziwe Wopatsayo. Yesu Mwini anapemphera kwa Atate, “Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Khristu amene munamtuma” (*Yohane 17:3*).

Cholinga chimodzi chachikulu cha kupemphera ndiko kuti timudziwe Wopatsayo. Mulungu si wamatsenga yemwe ali mlengalenga, yemwe akudikira kuti akwaniritse zokhumba zathu komanso agwetse madalitso a mvula. Iye akudikira chikondi, kudzipereka, ndi kupembedza kuchokera kwa ife. Ichitu n’chifukwa chake Salmo 37:4 likuti, “Udzikondweretse mwa Yehova; Ndipo Iye adzakupatsa zokhumba mtima wako.”

Chinsinsi Chakhumi ndi Chiwiri: KUPEMPHERA MOLIMBIKA MTIMA

Pomaliza, ngati tikufuna kuti mapemphero athu aziyankhidwa, tipemphere molimbika mtima ndi mosafoka. Tisaleke kupemphera pomati tatopa kapena pamene tikuona ngati kuti palibe chiyembekezo choti mapempherowo athuwo ayankhidwa, koma tipempherebe mpaka tiyankhidwe ndi kumvetsetsa yankho la pempherolo. Mzimu Woyera amatiuza kuti, “Kulimbika mu pemphero ndi njira yokhaya yomwe mapemphero athuwo angayankhidwe.”

Ichi ndi chifukwa chake Yesu akutilangiza ife kuti “Pemphani. . . Funani. . . Gogodani. . . (*Mateyu 7:7*) ndipo tipitiribe kugogoda! Nchifukwa chake mkazi wamasiiye uja pempho lake linamvedwa ndi woweruza wosalungama mu Luka 18. Mkaziyu analimbika mtima ndipo sanasiye kugogoda, kulimbika mtima uku ndi kumene Mulungu akufuna kuti kukhale mwa ife-tikhale anthu amene sitifoka, ndipo tigogodebe!

Mlongo Ellen White analemba mawu awa anzeru, “Palibepo choopsa kuti Mulungu amanyanyalanyaza kusayankha mapemphero ena a anthu Ake. Koma choopsa ndi chakuti anthuwo ayasedwe, kugwetsedwa mphwayi nasiya kulimbika kupemphera.”

Sikuti Mulungu akulipanga pemphero kukhala lovuta kapena lovuta kumvetsa kwa ife ayi. Iye akufuna anthu amene akumufunitsitsa lyeyo kwambiri, mwakuti anthuwa akangomupeza Iye, adzamutsata mpaka kale.

[Gawanani ndi anthu za zomwe zinakuchitikirani zokhudza kuyankhidwa kwa pemphero]

Tiyeni tipemphere kuti mitima yathu ikhale yozikika mu pemphero. Tifunse kwa Mulungu mvumbi wa madalitso amene Iye akudikira kuti atsanulire pa iwo amene akuwerenga Mawu Ake ndi kumumvera! Tiyeni tigwade ndi kupemphera moona mtima!

-Mapeto a Sabata Skulu-

Maphunziro

Mtima Umene Mulungu Amondwera Kukhalamo

[Ubwino wa Kusweka ndi Kudzichepetsa]

Wolemba: Melody Mason

Ndondomeko ya Chilinganizo (Tangoyerekeza mukhoza kusintha)

Lemba Lotsogolera: Yesaya 57:15

“Pakuti atero lye amene ali wamtali wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lake ndiye Woyera, ‘Ndikhala m’ malo atali ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzichepetsa, kutsitsimutsa mtima wa osweka.’”

Pemphero

Nyimbo Yapadera (mukhoza kuimba kapena ayi)

Mutu wa Maphunziro: “Mtima Umene Mulungu Amakondwera Kukhalamo”

Nthawi ya Mapemphero: Mupemphere kutengera Lemba lomwe tawerenga, “Ubwino wa Kudzichepetsa”

Kuumba mkota ndi Kutsiriza

Nyimbo Yomariza: 316, “Live Out Thy Life Within Me,” *Seventh-day Adventist Hymnal*

Pemphero

Mtima Umene Mulungu Amondwera Kukhalamo

[Ubwino wa Kusweka ndi Kudzichepetsa]

Wolemba: Melody Mason

Kodi munayamba mwaganizirako za mtima umene Mulungu amakondwera kukhalamo?

Baibulo limatiuza kuti, “Pakuti atero Iye amene ali wamtali wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lake ndiye Woyera, ‘Ndikhala m’ malo atali ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzichepetsa, kutsitsimutsa mtima wa osweka.’” (Yesaya 57:15).

Tikamawerengera Malemba, mobwereza-bwereza timapeza kuti Yehova amakondwera kukhala mu mtima umene ndi wosweka ndi wodzichepetsa. Kodi izi ndi chifukwa choti Mulungu amasangalala kutiona tikulira? Ayi! Ndi chifukwa choti mtimawo ndi osweka komanso wodzichepetsa ndipo anthu a mtima otere amadziwa kuti akusoweke Mpulumutsi, ndipo sanyada kuphunzitsidwa.

Mwatsoka, anthu onyada amavutika kuti asendeze chifupi ndi Mulungu. . .

Mbusa wina anati, “Munthu wonyada samva za ena, nthawi zonse amazitenga kukhala wodziwa.”

Munthu winanso analemba kuti, “Kunyada ndi nthenda yokhayo imene imapangitsa aliyense kudwala kupatula mwini nthendayo! (wonyadayo)

Mkulu winanso anati, “Kunyada ndi chotsatira cha tchimo. Kunyada kumamupha munthu pang’ono-pang’ono koma iye sadziwa.”

Ndikukhulupirira kuti zitsanzo zalembedwazi zokhudza kunyada, mukhoza kuzilumikiza ndi munthu wina amene mukumuganizira m’ moyo mwanu amene mukufunitsitsa akanamva uthengawu panopa. Koma maphunziro ano si okhudza munthu wina wake amene sali pano-maphunzirowa ndi okhudza inu ndi ine! Tikuyenera kumadzifunsa tokha kuti, “Kodi pali kunyada kwina mu mtima mwanga komwe kukuchititsa kuti Mulungu asandidalitse?”

Ndime ili m’ munsiyi kuchokera m’ bukhu la *Steps to Christ* yafotokoza zinthu molondola ndipo ikutithandiza ife kumvetsetsa mwakuya za chifukwa chimene nkhani yokhudza kunyada ili yofunikira kwambiri m’ moyo wa wokhulupirira:

“Ngakhale kunyada kukhoza kuoneka ka chinthu kakang’ono kapena kulakwika kumene kukuoneka kochepe pamaso pa anthu, palibe tchimo lomwe ndi laling’ono pamaso pa Yehova. Munthu amaona zinthu molakwika ndi mokondera, pomwe Mulungu amaona mmene zinthu zilili. Woledzera amadzudzulidwa nauzidwa kuti sakalowa kumwamba chifukwa chomwa mowa; ***pomwe kawiri-kawiri kunyada, kudzikonda, ndi kusirira sizimadzudzulidwa.*** Koma awatu ndi machimo amene amamupweteka Mulungu kwambirinso; kamba koti ndi otsutsana ndi khalidwe Lake lokoma mtima, Iye amapereka chikondi chosadzikweza kwa anthu okugwa padzikoli. Munthu yemwe amagwa m’machimo a mnanu akhoza kumaziimva kuti ndi wolakwa, wozingwa ndi wosowekera chisomo cha Khristu, koma wonyada samazimva kukhala wosoweka chisomo cha Khristu, kunyadaku kumatseka mtima wa Khristu ndi madalitso opanda malire amene Iye anadza kudzapereka kwa anthu.”

Kodi mukukumbukira zomwe taphunzira cha kummawaku? “Pempho lathu lokhalo lopita kwa Mulungu ndilo loti atipatse chifundo chomwe chili chosowa chathu chachikulu.” Tsono, ngati mu kudzichepetsa kwathu timazindikira kuti ndife osowa, ndiye kuti tili ndi chiyembekezo!

Musaiwale, ngati mukumva kukhala ogonjetsedwa, kuzimva kuti muli mu chipululu cha uzimu chafumbi ndipo simukudziwa kuti mutulukamo motani, ngati ndi choncho Mulungu akudikira inu kuti agwire nanu ntchito! Yehova amakonda kugwira ntchito ndi dothi komanso mafupa ouma.

Yesu akutiiza kuti, “Sindinadza Ine kuitana olungama, koma ochimwa kuti atembenuke mtima” (*Luka 5:32*). Tikazindikira kuti ndife ochimwa, ndiye kuti tipeza chilimbikitso, chifukwa choti tili oyenera kulandira mphatso ya chipulumutso.

Tikabwerera ku nkhani ya kudzichepetsa, ngati Mulungu akutiina kuti tikhale ndi khalidwe lodzichepetsa, kodi khalidweli limakhala lotani tsiku ndi tsiku?

M’bukhu la *Continuous Revival: The Secret to Victorious Living*, mlembi wa bukhu Norman Grubb analembe mawu awa:

Maubwenzi onse Achikhristu ali mbali ziwiri. Mbali ina ndi *yokhotakhota* pomwe ina ndi *yoongoka*. . . Mwa chitsanzo, sitinganene kuti ndife olungama pamaso pa Mulungu kupyolera mwa Khristu kwinauku nkukhala anthu osalungama pamaso pa anthu anzathu.

Ndinene motere. Tikhoza kumuyerekeza munthu ndi nyumba. Nyumba imakhala ndi denga komanso makoma, nayenso munthu wokugwa amakhala ndi denga pamwamba pa machimo ake, lomulekenitsa iye ndi Mulungu; ndipo munthuyu alinso ndi makoma omwe amamulekanitsa iye ndi mnzake woyandikana naye. Koma pa chipulumutso, ali wosweka pa mtanda, sikuti denga la munthuyu limachoka chifukwa cha kukhulupirira mwa Khristu, koma makomawonso amagwa, ndipo munthuyu amavomereza pamaso pa anthu onse kuti iye anali wochimwa koma wapulumuka mwa chisomo.

Tsoka ilo, munthuyu akangotembenuka mtima-pamabwera chotchinga cholepheretsa kuti pasakhale kupitirira kwa kutsitsimuka. Kupitirira kwa kutsitsimuka ndi kupitiriranso kwa kusweka; koma kusweka kuli mbali ziwiri, zomwe zikutanthauza kuti makoma a nyumba ija akuyenera kugwetsedwa komanso denga kuchotsedwa. Koma tchimo la munthu lalikulu ndi loipa kwambiri ndi tchimo la kunyada: kudzikondweretsa wekha ndi kudzitukumula. Ngakhale sitizindikira izi, pamene tikuonetsetsa kuti pasakhale chotchinga/denga pakati pa ife ndi Mulungu kupyolera mu kulapa ndi kukhulupirira,

posakhalitsa timabwezeretsanso makoma otitchinga ife ndi anzathu aja. Sitalabadira za anzathuwa chifukwa choti timakhala tikukondwera ndi chipambano chomwe tapeza pokhale ife Akhristu. Tikapindula moyo, kuphunzitsa pa kalasi, pemphero lathu likayankhidwa, tikapeza mfundo zina kuchokera m’Malembo-sitalabadira za zimene anthuwa amamva zokhudza zinthuzi, chifukwa choti timatangwanika ndi kuyamikiridwa komwe ena akutiyamikira.

Ngati Mulungu akufuna kuchita ndi kusaleza mtima kapena mkwiyo wathu kunyumba, kapena kusakhulupirika kwathu pa bizinesi, nkhwidzi kapena tchimo linalake, mosakaikanso zikatele ife timachitira umboni kwa abale ndi alongo za kukhulupirika kwa Mulungu komanso machitachita Ake okoma mtima kwa anthu ochimwa. Nkulekeranji? Chifukwa cha kunyada basi. . . Tchutchutchu ndi wakuti, anthufe timafuna ulemmerero wa anthu komanso wa Mulungu, ndipo izitu ndi zimene Malembo amanena kuti zimachititsa anthu kusiya kumuvomereza Mulungu pamaso pa anthu anzawo (*Yohane 12:42-43*).

A Andrew Murray m’bukhu lawo lotchedwa *Humility and Absolute Surrender* akuti, “N’kwapafupi kuganiza kuti ndife odzichepetsa pamaso pa Mulungu: koma kudzichepetsa pamaso pa anthu kudzakhala umboni wokhawo wokwanira kuti kudzichepetsa kwathu pamaso pa Mulungu nkoona.”

Mlongo White nayenso akuti, “Mtima wonyada udzichepetse ndipo mtima wolimba usweke. Kudzikweza ndi kunyada kusakhalepo. Taonani, yang’anani kwa Iye amene anapyozedwa chifukwa cha machimo. Muoneni Iye akutsika pang’ono ndi pang’ono modzichepetsa kuti atikweze ife; kudzichepetsa koposa ndi cholinga choti atipulumutse tonsefe amene tinagwa chifukwa cha tchimo! Nanga timakhaliranjiki wosasamala, oipa mtima, onyada, ndi odzimva tokha kukhala okwanira kwambiri? Kodi ndi ndani mwa ife yemwe mokhulupirika akutsatira ndondomeko yofuna kuthana ndi makhalidwe oipa atchulidwa? Nanga kodi ndi ndani mwa ife wayamba ndipo akupitiriza nkondo yolimbana ndi mtima wonyada? Tsono ndi ndani mwa ife, amene mosweka mtima, akulimbana ndi kudzikonda mpaka ataonetsetsa kuti kudzikondako kuchoke mu mtima mwake komanso kusaonekere m’moyo mwake?”

Ndigawane nanu nthano!

Mtima Wosadzikweza

UMBONI WA CORRIE TEN BOOM

Mwina nkutheka munamvako za Mayi Corrie Ten Boom omwe, pamodzi ndi banja lawo, iwo anathandiza kupulumutsa miyoyo ya Ayuda oposa 800 nthawi ya kuphedwa kwa Ayuda pa nthawi ya Nkhondo Yachiwiri ya Dziko lonse Lapansi. Chifukwa cha ntchito yochitika mwakabisira yomwe banjali limachita ku Holland, banjali linamangidwa ndi kutumizidwa ku Ravensbrück, kumeneku ndi kumene anthu amachitiridwa nkhanza zosasimbika m’dziko lonse la Germany. Anthu zikwi-zikwi anaphedwa pamalowa.

Nthawi imene mayi Corie anatulutsidwa kuchoka pa malowa m’uwezi wa Disembala m’chaka cha 1944, anthu onse a pabanja pawo nkuti ataphedwa ku ndende. Ngakhale zinali motere, m’malo moti mayiwa akhale akudandaula komanso kukhala ndi khwidzi, iwo anayamba kuyenda dziko lonse lapansi kufalitsa uthenga wa chikondi cha Yesu.

Mayi Corie anali wodziwika komanso wokondedwa chifukwa cha kukoma mtima, chisomo, chifundo, ndi mtima wawo wodzichepetsa, ndipo ambiri anadza kwa Yesu chifukwa cha umboni wa Mayiwa. Chikhalirecho, mayiwa analitu munthu monga inu ndi ine.

Nthawi ina, Mayiwa anafotokoza za zimene anakumana nazo ku msonkhano wina kumene iwo ankalalikira madzulo m'dziko la Cuba. Iwowa anali atalalikira uthenga wokhudza chikondi cha Mulungu, ndipo amadikira abambo awiri kuti nawonso atsirize maualiki awo omwe anali atali-atali. Kunali kukutentha kwambiri komanso kunali chinyontho, utitiri woyabwa unali paliponse, ndipo kunja kunali kukuda. Mayiwa anatopa ndipo sakanatha kupiriranso chifukwa choti mlaliki wotsiriza amachedwa ndi kuitanira anthu kuti azipereke kutsogolo.

“Ayi ndithu ndikukhulupirira kuti palibe akusangalatsidwa ndi kudzipereka kwa Khristu pakadali pano, aliyense akufuna kupita kwawo. Bola aliyense asabwere kutsogolo kuzipereka. Ndikufunitsitsa ntakagona ine,” anadziyankhulira okha-okha mayiwa.

Koma chodabwitsa nchakuti anthu ambiri anayamba kukhamukira kutsogolo. Ena mwa anthuwa amalira. Mwadzidzidzi mayi Corrie anazindikira kudzikonda komwe kunali mu mtima mwawo. Poyamba ankafuna kuti anthuwa asapereke moyo wawo kwa Yesu usiku umenewo chifukwa choti iye anatopa komanso amamva kutentha. Mwansanga-nsanga anazindikira tchimo lawo kwa Mulungu namupempha iye kuti awakhululukire, kenano anadzuka nakapemphera limodzi ndi anthu aja anabwera kutsogolo.

Tsiku lotsatira, Mayi Corrie anapemphedwa kuti akalalike ku mpingo wina waukulu ku dera lina la anthu achuma ku Havana. Anthu ochuluka otchuka ndi achuma anabwera ku kudzamvera. Mayiwa akulowa m'tchalitchi m'mawa watsikulo, anapatsidwa kabukhu koofotokoza mbiri ya mayiwa koma inalembedwa mokokomeza. Mbiri inayamba ndi kuti: “Mayi Corrie Ten Boom ndi mlaliki wotchuka padziko lonse lapansi. . . Iwo amagwira ntchito molimbika, mosadzikonda ndi modzipereka pofalitsa uthenga wabwino.” Mayi atawerenga mbiriyi chamumtima, mtima wawo unanthunthumira, ndipo anapemphera chamumtima, “Ooo Ambuye, anthuwa akanadziwa zeni-zeni za khalidwe langa, sibwezi atandiitana kuti ndidzalalikire m'mawa uno.”

“N'chifukwa ninji sukuliuza dziko za khalidwe lako leni-teni. . .” Mzimu Woyera anawayankha motero Mayiwa. Mwansanga-nsanga a Corrie anayamba kumudandaulira Mulungu. “Koma Ambuye, ndikawauza anthuwa za khalidwe langa, akandikana zikhala motani?” Kachiwirinso, anamva mawu akayaziya koma amphamvu akuti, “Kodi Ine ndingadalitse bodza.”

M'mawa umenewo mayi Corrie anawauza anthu omwe amawamvetsera zoonza zeni-zeni za khalidwe lawo. Pachifukwa ichi, anthu ambiri mitima yawo inasweka ndipo umbo wawo unakhala maziko a kutsitsimuka kwakukulu.

Kodi Kusweka Koonza ndi Chani? Mwina mukhoza kumadzifunsa. Ena amaganiza kuti ndi kupitirira kwa kuziunguza mwakuya munthuyo ali wodandaula. Enanso amaganiza kuti ndi kutengeka kwamphamvu popemphera kapena kukhumudwitsidwa mu mzimu pamene munthu uli wokondwa. Pomwe ena amaganiza kuti ndi zokhudza kulolera kuchitiridwa nkhanza mwakabisira chaka ndi chaka. Zoonza zake ndi zakuti pa mfundo zonsezi palibepo yankho. Tchutchutchu ndi wakuti ambiri apirira nkhanza zochitiridwa mtseli, ndipo alira kwambiri, chikhalirecho iwo akumana ndi kusweka kweni-kweni.

Kusweka koonza ndi khalidwe lochitika nthawi-ndi-nthawi povomerezana ndi Mulungu za zeni-zeni zokhudza moyo komanso mtima wanga-osati zimene wina aliyense akuganiza koma zoonza nzimene akunena Mulungu. Kusweka ndi kusiya khalidwe langa lonyada-kusiya kotheratu chifuniro changa mu chifuniro cha Mulungu. Kusweka ndiko kuyankhula kuti, 'Inde, Ambuye'-palibe kukana, kuukira, kusamvera-m'malo mwake kudzipereka wekha [posatengera zokhoma ndi mavuto omwe ungakumane nawo] ku chitsogozo ndi chifuniro cha Yehova m'moyo mwanga.

Masana uno tikhala ndi nthawi yopemphera ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize ife kuti mkati mwathu mukhale kusweka koono, ndi kuzindikira chosowa chatu cheni-cheni cha uzimu.

Mapemphero athu gonera pa kuwerenga za “**Ubwino wa Kudzichepetsa.**”

Tsopano ndikuchenjezeni, zomwe tiwerenge masana uno musazitenge mwamasewera chifukwa choti zimachekeka! Mtima wanga unachekeka pamene ndinawerenga koyamba za izi kamba koti ndinazindikira kuti ndikusowekera chisomo cha Mulungu chopulumutsa. Ichi n’chifukwa chake ndaona kuti nkofunikira kugawana nanu.

Mawu achilimbikitso akutiiza kuti, “Nthawi zambiri tikuyenera kugwada ndi kulira pa mapazi a Yesu, chifukwa cha zofooka ndi zolakwika zathu; koma sitikuyenera kugwetsedwa mphwayi. . . . Pamene tasiya kukhulupirira mphamvu yathu, tikuyenera kukhulupirira mphamvu ya Mombolo wathu.”

Kumbukirani, Yesu ali nafe, ndipo lye akutisendeza chifupi ndi mtanda. *Ndipo awa ndiwo malo abwino kwambiri kukhala!*

Ubwino wa Kudzichepetsa

PEMPHERO LOWERENGA

Mfundo Zothandizira Nthawi ya Mapemphero:

Mukhoza kutsatira mfundo zotsatirazi.

1. Anthu awiri akhoza kuwerenga kutsogolo mbali zingapo pa mutu wa “Ubwino wa Kudzichepetsa”. Wina awerenge mbali ya KUDZICHEPETA, wina mbali ya KUNYADA. Kenako anthu akhoza kukhala mu timagulu kupempherera mfundo zomwe zawerengedwa.
2. Wotsogolera akhoza kuwerenga mbali zingapo pa mutu wa “Ubwino wa Kudzichepetsa” kutsogolo kenako atsogolere pemphero la chimvano kwa mphindi zochepe popempherera mfundo zomwe zatchulidwa, ndipo nonse mupemphere pamodzi, kenako mubwereze mapemphererowa mpaka mutamaliza mfundo zonse.
3. Wotsogolera akhozanso kuwerenga nkhani yonse yokhudza “Ubwino wa Kudzichepetsa” kenako mupereke nthawi ku magulu kuti akambirane ndipo kumapeto apemphere.
4. Mtsogolera akhozanso kupereka nkhani yokhudza “Kunyada” ndi “Kudzichepetsa” ndi kulora magulu aja kuti awerenge ndi kupemphera. Kapena pemphani anthu kuti apemphere pawokha.

MFUNDO YOFUNIKIRA: Pamene tamva kutsutsika chifukwa cha tchimo lina, ndi kwabwino kupemphera.

Ubwino wa Kudzichepetsa

[Kusiyana kwa Pakati pa Kunyada ndi Kudzichepetsa]

KUSIYANA

- **Anthu onyada ndi odzimva amaona kuti zabwino zonse zomwe amachita ndi zowayenereza kupeza Chipulumutso.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amadziwa kuti ndi kupyolera mu chilungamo cha Khristu chokha m'mene iwo angapeze Chipulumutso.

“Zosati zochokera m'ntchito za m'chilungamo, zimene tidzachichita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera” (Tito 3:5).

- **Anthu onyada ndi odzimva amadzikhululupirira okha ndi kudzitamandira chifukwa cha zimene amadziwa.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amavomereza kuti pali zinthu zina zomwe akuyenera kuti aphunzire.

“Pomwepo Davide mfumu analowa, nakhala pansi pamaso pa Yehova; nati, Ine ndine yani, Yehova Mulungu, ndi banja langa ndi chiyani kuti munandifikitsa pano?” (2 Samueli 7:18).

- **Anthu onyada ndi odzimva amathokoza Mulungu kuti iwo sali monga ena owazungulira.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amazindikira kuti “kunyada” pakokha ndi tchimo loopsa monga zilili ndi machimo ena onse.

“Yense wonyada mtima anyansa Yehova; Zoonadi sadzapulumuka chilango” (Miyambo 16:5).

- **Anthu onyada ndi odzimva amasunga udani chifukwa choti amalephere kunena kuti, “Pepani ndinakulakwirani. Kodi mungandikhulukire?”**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda sazengereza ponena kuti, “Pepani, tiyeni tikhulukirane ndi kuyanjana.”

“Chifukwa chake ngati ulikupereka mtulo wako pa guwa la nsembe, ndipo pomwepo ukakumbukira kuti mbale wako ali ndi kanthu pa iwe, usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nuchoke, nuyambe kuyanjana ndi mbale wako, ndipo pamenepo idza nupereke mtulo wako” (Mateyu 5:23, 24).

- **Anthu onyada ndi odzimva amayang'ana zofooka ndi zolephera za ena ndipo salabadira za kusweka kwa ena.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amadzimvera chisoni chifukwa cha zofooka zawo ndi chosowejera chawo chachikulu cha uzimu ndipo amamvera chisoni iwo omwe ali osweka.

“Mauwa ali okhulupirika ndi oyenera konse kuti awalandire, kuti Yesu Khristu anadza ku dziko lapansi kupulumutsa ochimwa; wa iwowa ine ndine woposa” (1 Timoteo 1:15).

- **Anthu onyada ndi odzimva amafuna kuonetsera kwa anthu kuti akulondola ngakhale akudziwa kuti ndi akulakwa.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amangochita zolondola sachita kuonetsera kwa anthu, amafunitsitsa kwambiri kukhala olondola/olungama pamaso pa Mulungu koposa pamaso pa anthu.

“Pakuti, kumva zowawa chifukwa cha kuchita zabwino, ndi kumva zowawa chifukwa cha kuchita zoipa, nkwabwino kumva zowawa chifukwa cha kuchita zabwino, ngati chitero chifuniro cha Mulungu (1 Petro 3:17).

- **Anthu onyada ndi odzimva amalabadira za zochita zawo, nthawi, ndi khalidwe lawo.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amakhala ndi mtima wopatsa komanso amalolera kuti Mulungu atenge ulamuliro wa zochita, nthawi, ndi khalidwe lawo.

“Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokuchumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani m’manja mwanu. Pakuti kudzayesedwa kwa inu ndi muyeso womwewo muyesa nawo inu” (Luka 6:38).

- **Anthu onyada ndi odzimva salabadira zothandiza anthu otsika, iwo amene alibe mwayi wopeza zinthu zina.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda nthawi zonse amafunitsitsa kuthandiza ndi kutumikira ngakhale kwa “ang’onong’ono awa” monga anachitira ndi Yesu

“Ndipo Mfumuyo idzayankha nidzati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, Chifukwa munachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale ang’onong’ono awa, munandichitira ichi Ine” (Mateyu 25:40).

- **Anthu onyada ndi odzimva amafunitsitsa atatchuka ndi kuyamikiridwa, ndipo amakhala ndi njala yofuna kupambana mipikisano, zikho ndi mphotho.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amafunitsitsa kukhala okhulupirika kuti ulemerero wa Yehova uonekere, ndipo amapeza kufuna kutchuka kapena kuyamikiridwa.

“Kwa ife ai, Yehova, kwa ife ai, Koma kwa dzina lanu patsani ulemerero, Chifukwa cha chifundo chanu, ndi choonadi chanu” (Masalmo 115:1).

- **Anthu onyada ndi odzimva amaonetsera kwa anthu maudindo komanso zomwe akwaniritsa m’ moyo ndipo amamva kuti akuyenera kulandira ulemu wapaderadera.**

- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda saonetsera maudindo komanso zomwe akwaniritsa, amavomereza kusachita zinthu mosaonetsera m'malo mwake ulemerero upite kwa Mulungu.

“Anthu ambiri abukitsa yense kukoma mtima kwake; Koma ndani angapeze munthu wokhulupirika?” (Miyambo 20:6).

- **Anthu onyada ndi odzimva amagwiritsa ntchito moyo wawo komanso chikoka choka chomwe ali nacho monga mwayi woti azionetsere okha kwa anthu.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amagwiritsa ntchito mwayi ndi chikoka chomwe Mulungu wapereka kwa iwo pokweza Khristu ndi kuonetsetsa kuti Khristu yekhayo aonekere.

“Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe” (Yohane 3:30).

- **Anthu onyada ndi odzimva amaona kukhala chovuta kutumikira ndi kugonjera ena, ndipo amakonda kudzudzula ndi kudandaula motsutsana ndi awo omwe ali olamulira kapena ndi atsogoleri.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda, monga Yesu, amatumikira anthu onse modzichepetsa, posatengera kapezedwe kachuma kapena udindo wa otumikiridwawo. Anthu odzichepetsa ndi osadzikondawa amakweza iwo amene sakuyembekezera phindu lililonse kwa iwo, komanso amalekeza iwo amene ali pa ulamuliro.

“Ndipo amene aliyense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la anthu ambiri” (Mateyu 20:27, 28).

- **Anthu onyada ndi odzimva nthawi zonse amaganiza za zinthu zabwino zomwe amamuchitira Mulungu, anthuwa amaganizanso kuti mpingo kapena utumiki sungayende popanda iwo.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amazindikira kuti popanda Yehova, iwo sangachite kanthu kalikonse kaphindi mu Ufumu Wake. Amachimva kukhala chinthu chamwayi kuti Yehova akuwagwiritsa iwo ntchito.

“Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu” (Afilipi 2:13).

- **Anthu onyada ndi odzimva kawiri-kawiri amakhala oipa mtima, ankhanza, osakhululuka ndi osafikirika. Pakakhala kusamvetsetsana, iwo amadikira kuti ena ayambe kuchitapo kanthu pobweretsa chiyanjano.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amakhala okoma mtima, achikondi, a khalidwe labwino, okhululuka, ndi osavuta kuwapempha kanthu. Anthuwa amakhalanso amachawi kuyanjana ndi ena zinthu zikalakwika.

“Chiwawo chonse, ndi kupsya mtima, ndi mkwiyo, ndi chiwawa, ndi mwano zichotsedwe kwa inu, ndiponso choipa chonse. Koma mukhalirane okoma mtima wina ndi mnzake, a mtima wachifundo, akukhululukirana nokha, monganso Mulungu mwa Khristu anakhululukira inu” (Aefeso 4:31, 32).

- **Anthu onyada ndi odzimva kawiri-kawiri amaziikira kumbuyo akadzudzulidwa, ndipo safuna kuti ena adziwe kuti iwo alakwitsa.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amamva chidzudzulo ndi mtima wofatsa ndipo amafunitsitsa kuti achite bwino. Sakhala odandaula pamene ena awona zofooka mwa iwo.

“Pakuti Yehova adzudzula omwe awakonda; Monga atate mwana amene akondwera naye” (Miyambo 3:12).

- **Anthu onyada ndi odzimva amakonda kuchita zinthu pawokha ndipo safuna kugawana ndi ena mavuto ndi zosowa zawo za moyo wauzimu.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amamasukira ena powauza za mavuto awo, sakhala ovuta ndipo amanena chilungamo. Iwo sakhala okhudzika kuti akuoneka ofooka, koma amafunitsitsa kuoneka oona ncholinga choti mphamvu ya Mulungu ithe kukwezedwa ngakhale mu nyengo zimene pali kufoka.

“Ndipo ananena kwa ine, Chisomo changa chikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m’ufoko. Chifukwa chake makamaka ndidzadzitamandira mokondweratu m’maufoko anga, kuti mphamvu ya Khristu ikhale pa ine” (2 Akorinto 12:9).

- **Anthu onyada ndi odzimva, polapa machimo awo kwa Mulungu, iwo sanena machimowo mmalo mwake amangopemphera mwachidule. “Wokonedwa Ambuye Mulungu, chonde mundikhululukire machimo anga onse.”**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda, nthawi zonse akamalapa machimo awo kwa Yehova amanena mwatchutchutchu. “Wokonedwa Ambuye Mulungu, chonde ndikhululukireni chifukwa nda_____.”

“Chifukwa chake muvomerezane, wina ndi ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m’machitidwe ake” (Yakobo 5:16).

- **Anthu onyada ndi odzimva amafuna kupatsidwa ulemu osati iwowo kukhala chitsanzo chabwino kwa anthu, ndipo kawiri-kawiri amakhala moyo wodzimva kuti ndi wolungama.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amatangwanika ndi kuchita zolungama pamaso pa Mulungu, ndipo amapewa makhalidwe onse a chinyengo komanso osiyana ndi zimene iwo amayankhula.

“ Pakuti Yehova saona monga aona munthu; pakuti munthu ayang’ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang’ana mumtima” (1 Samueli 16:7).

- **Anthu onyada ndi odzimva amadziyerekeza okha ndi ena ndipo amadzimva kukhala woyenera kulandira ulemu ndi chipulumutso.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amazindikira kuchimwa kwawo, ndipo amatamanda Mulungu kuti iye anatumiza Mwana Wake kuti, ngakhale munthuyu samayenera kulandira chipulumutso, iye akhoza kulandira chipulumutso ndi ulemu.

“Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife” (Aroma 5:8).

- **Anthu onyada ndi odzimva amaganiza kuti alibwino, koma sadziwa zeni-zeni za mu mtima mwawo.**
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda nthawi zonse amati “Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa”

“Koma wansonkhoyo alikuima patali sanafuna kungakhale kukweza maso kumwamba, komatu anadziguguda pachifuwa pake nanena, Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa” (Luka 18:13).

- **Anthu onyada ndi odzimva amaganiza kuti sakusowekera chitsitsimutso, koma anthu ena ndiwo akusowekera chitsitsimutso osati iwowo ayi.** (Mwakuti, tikunena pano, anthu onyadawa, m’aganizo mwawo akukonza mndandanda wa anthu onse omwe akusowekera chitsitsimutso.)
- Anthu odzichepetsa ndi osadzikonda amakhala oyambirira kuvomereza kuti akusowekera chitsitsimutso chauzimu! Nthawi zonse amafunitsitsa kuti Mzimu Woyera atsanulidwe m’mitima ndi m’miyoyo yawo.

“Kodi simudzatipatsanso moyo, Kuti anthu anu akondwerere ndi Inu?” (Masalmo 85:6).

“Mundichitire chifundo, Ambuye; Pakuti tsiku lonse ndiitana Inu” (Masalmo 86:3).

[M’maphunziro a masana mukhale ndi nthawi yopempherera chiyang’aniro cha mapemphero a chaka chino, komanso za “Ubwino wa Kudzichepetsa.” Kenako mumalize chilinganizo.]

Kutsiriza Chilinganizo Pambuyo Pakumariza Kupemphera:

Kodi tinganene kuti LEMEKEZANI YEHOVA, kuti ife timatumikira Mulungu yemwe angathe kuperekanso moyo kwa mafuna owuma?

Timatumikira Mulungu yemwe akhoza kusintha mitima! (Ezekieli 36:26)

Ifetu timatumikira Mulungu yemwe akhoza kuchotsa mtima wonyada ndi kuupanga kukhala wabwino ndi wodzichepetsa!

Mobwerezanso..... tiyeni timupatse Mulungu dothi lathu!

Monga taphunzira masana uno, pali malo awiri amene Mulungu amakhala. . . malo oyamba ndi kumwamba komwe ndi koyera, kwina ndi mu mtima wosweka ndi wolapa-mtima wodzichepetsa!

Palinso malo ena amene sitinawatchule, kumene Yehova amakondwera kukhalako! Iye amakondwera kukhala m'mitima ya iwo amene amalemekeza dzina Lake!

Baibulo likuti, Yehova amakhala m'matamando a anthu Ake!

Pamene tikutseka chilinganizo chathu masana uno, tiyeni timutamande Mulungu kuti iye watipatsa zonse zomwe tisowa pa moyo ndi chipembedzo. . . . Zoipa zimene mdani wakonza, Mulungu akhoza kuzisandutsa kukhala zabwino.

Chisomo kwa inu ndi mtendere zichulukitsidwe m'chidziwitso cha Mulungu ndi Yesu Ambuye wathu. Popeza mphamvu ya umulungu wake yatipatsa ife zinthu zonse zapamoyo ndi chipembedzo, mwa chidziwitso cha Iye amene adatiitana ife ndi ulemerero ndi ukoma wake wa Iye yekha; **mwa izi adatipatsa malonjezano a mtengo wake ndi akulu ndithu**; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nawo umulungu wake, mutapuluma ku chivundi chili pa dziko lapansi m'chilakolako (*2 Petro 1:2-4*).

-Mathero a Chilinganizo cha Lasabata Masabata-